


NTCHITO NDI

CHIKHULUPIRIRO

CHOFOTOKOZEDWA

 Zikomo inu. Ndi zabwino kukhala pano, usikuuno, kachiwiri. Ine sindinadziwe kuti iwo anadziwa bwanji kuti ine ndipempherera odwala. Aliyense wabwera kuti adzapempheredwe. Inu mukudziwa, ine ndikukhulupirira ngati inu mukutsatira kutsogolera kwa Mzimu, izo zonse ziri bwino. Ndizo zabwino kwambiri, umenewo ndiwo Uthenga umene sumalephera konse.

² Tsopano, ine ndinali nditakhala mchipinda lero, zitatha . . . mtumiki wina yemwe ali wokonedwa kwambiri ku mtima wanga (atatu a iwo), atatu mwa abwenzi anga abwino enieni, iwo anandiuza kuti akubwera kudzadya nkhomaliro ndi ine. Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, izo zinali basi zabwino,” inu mukudziwa.

³ Kotero ine—ine ndimangodya kadzutsa pang’ono chifukwa ine ndinali wotsimikiza kuti iwo anali oti azilipira izo, inu mwawona, ndipo ine . . . ndiri ndi chakudya chamadzulo chabwino chathunthu. Kotero 12:00 inafika, ndipo 1:00 inafika, ndipo 2:00 inafika, panali palibe aliyense apobe. Kotero apo panali . . . apolisi anali kuthamangitsa chigawenga, kumusi uko pabwalo, ndipo kotero ine ndinapita uko kuti ndikawone chochitika chimenecho. Ine sindinathe kumupeza nkomwe M’bale Jack. Kotero, ine ndinadzapeza kuti, bambo wa hoteloyo anali atamupatsa iye nambala yolakwika; ndipo iye anali kuyimba pa chitseko cholakwika, nthawi yonseyo, kumene ine—ine kunalibeko. Ine ndidzamulola iye kuti andilipirire ine, kamodzinso, komabe, nthawi ina. Iye ndi M’bale Tracy, ine ndinali wokondwa ndithudi kuwawona iwo ndi M’bale Brown usikuuno. Izo zikungowoneka ngati kuti ife tikuyenera kubwerera ku Arizona kachiwiri.

⁴ Ine ndikukhoza kukumbukira ndikubwera kudutsa chipululu tsiku lina. Ine ndinamuza mkazi wanga, kumbuyo uko, ine ndinati, “Apa ndi pamene M’bale Jack anakhala kumbuyo kwa Chevrolet yaing’ono iyi.” M’bale Brown ndipo iye anakutsa zonse za—chilengedwe chapachiyambi, kaya izo zinachitika mmasiku sikisi kapena kaya izo zinachitika mu zaka sikisi miliyoni. Izo zinali zabwino.

⁵ Iwo amatsutsana kwambiri, iwo anatuluka panja ndi

kutenga miyala yodzadza manja, ndipo wina amapita kukayima kuseri kwa mtengo umodzi, ndi wina unzake, ndi kumaponyerana miyala pa wina ndi mzake molimba basi momwe iwo angathere. Iwo sakanakhoza kuzithetsa izo mwanjira imeneyo, kunena, “Ine ndikhoza kukuposa kuthamanga.” Kumusi kwa msewu iwo amatha kupita; M’bale Jack, munthu wamng’ono wamfupi, molimba basi monga iye akanakhoza kuzipotokolera; ndipo M’bale Young ndi miyendo yayitali imeneyo, inu mukudziwa. Ine sindinasekepo kwambiri mmoyo wanga!

⁶ Kenako, M’bale Jack anabwerera mgalimoto ndipo anavula nsapato zake. M’bale Sharrit anali atatipatsa ife thumba lalikulu la malalanje, ndipo iye anadya theka la iwo ife tisanafike ku Shreveport.

⁷ Inu mukudziwa, amenewo ndi masiku agolide, ngakhale. Inde, bwana, iwo ndi masiku agolide. Ine ndikudziwa izo zikumveka mwanthabwala, moseketsa, koma ndi zoono. Koma ife...pali chinachake cha izo, iwe ukamakalamba izo zimayamba kuyendayenda m’malingaliro ako. Iwe umaganiza za masiku amenewo omwe iwe umalalakala utawakhalanso kachiwiri, ndiko kulondola, masiku aubwana wathu. Ndipo pamene ife tikukalamba, izo zonse zimasanduka zithunzi. Ndine wokondwa kuti izo zinali zangwiro ndi zojera, ndi chiyanjano cha paabale, mu chikondi. Podziwa kuti ife tikupita ku Dziko kumene ife sitidzakalamba konse, kumene...Dziko lalikulu lija, uko, kumene ife, sitidzakalamba konse kapena kufa konse.

⁸ Mmodzi wa abale athu ofunika, wokondedwa kwambiri kwa ife tonse, iye wangowolokera kumene mu Dziko limenero. Ndipo nthawi iliyonse ine ndikabwera pa nsanja iyi, ine—ine ndikuganiza ine ndiziganiza za M’bale Lyle. Ine ndinayang’ana uko usiku watha ndipo ndinamuwona Judy wamng’ono atakhala pamenepo, ndipo mtima wanga umangogunda, ine ndinali kuganzirira mmene iye ankamverera. Ndipo ine ndikudziwa pamene adadi anamwalira mmene...Koma ife timangoyenera kudutsa m’masukulu amenewo a kuvutikawo kuti tidziwe mmene munthu winayo akumvera.

⁹ Ine ndikukhulupirira ine ndikuyang’ana pa mtumiki mzanga wakale wakhala apa. Ine sindingathe basi kumutchula iye. Ndi kulondola uko, inu munkakonda kumapempherera odwala kuno, nthawi zonse, zaka zapitazo? Hierholzer, limenero—dzina la chi German limenero, ine sindikanakhoza kulitchula ilo bwino basi. M’bale Tracy, ine ndinakumana naye kunja uko. Ndipo ine ndinamudziwa iye pafupifupi zaka teni, ndipo ine ndinati, “Inu simunakule ndi miyezi sikisi mu zaka teni zimenezo.” Ife tikukhala mu dziko limene liyenera kutha tsiku lina.

¹⁰ Tsopano, usikuuno, ine ndinali...Ndinikusungani inu mochedwa kwenikweni usiku wathawu, ine ndiyesera kuti

ndisachite izo usikuuno. Kuti ndimalize nkhani yanga... Ine ndimaganiza zokhudza, usikuuno, kulalikira pa phu-phunziro la *Mkwatulo*, kwa mpingo. Momwe zikhalidwe, pamene ine ndikuziwona izo mu Lemba, zikhalidwe zomwe Mpingo ukuyenera kuti udzakhalemo kwa *Mkwatulo*, ndi chimene chiti chidzachitike basi *Mkwatulo* usanachitike, ndi momwe icho chidzachitikire. Ndipo ife tonse timakhulupirira mu *Mkwatulo*, sichoncho ife? Ife timakhulupirira mwa Iwo. Ndipo kenano, zonse pakamodzi, Chinachake chinangoti, “Upempherere odwala, usikuuno.” Ndipo ine ndinali nditangodya kumene chakudya chamadzulo ndi m’bale wamng’ono wachi Mexico kumeneko, ine ndinapita uko ndipo ndinakamutenga iye pa msewu. Ine ndikuganiza iye ali pano usikuuno, iye ndi mkazi wake.

¹¹ Ndipo kenako winawake anabwera, anadzandipatsa ine umboni. Anati, “Ngati... Pabwalo kapena kutchalitchi,” iye anati, “kuli mwamuna kumeneko, yemwe, ine ndikukhulupirira izo zinali pafupifupi chaka chapitacho, kuti iye anafika mu mzere wa kuzindikira.” Ndipo ine ndimaganiza, usikuuno, zongokhala ndi mzere wa pemphero wachikale, monga M’bale Jack ndi M’bale...

¹² M’bale Young Brown anakonda kundiperekera ine makadi a pemphero. Ndipo ine ndinamupeza iye woonamtima kwenikweni ndipo sindinamugwirepo iye akugulitsa khadi kapena akuchita chirichonse cholakwika, iye ndi wowongoka kwenikweni. Ndipo ife tawagwirapo iwo akuyesera kuti achite zimenezo, inu mukudziwa. Kotero—kotero ife... M’bale Young, iye anali pa ntchito nthawi zonse, ndipo wokhulupirika. Ndipo ine ndikukumbukira, iye anakonda kuyima ndi kutenga makadi, ndi kumawabweretsa iwo kudutsa mu mzere. Ine ndinkawapempherera iwo ndipo iwo amapita modutsa, basi chikhulupiriro chosaipitsidwa icho chimene anthu amenewo anali nacho, ngati iwo angangoyandikira pafupi ndi inu iwo ankachira. Ndipo ine ndikuganiza apo panali machiritso twente ku amodzi, kwa omwe ife tiri nawo tsopano.

¹³ Ndiye, nkhani iyi inabwera madzulo ano ya munthu, iye mwinamwake ali pano tsopano. Kuti iye anali mu mzere wa pemphero, chaka chapitacho, kwinakwake, ndipo—ndipo iye anali... anati, mu kuzindikira anauzidwa kuti iye anali ndi masagwidi. Ndipo madokotala anamuuzza iye, masagwidiwo atagwa, kuti iye sakanakhoza kukhala ndi mwana wamkazi, ndipo iye nthawizonse amamufuna iye. Ine ndikuganiza iye anali ndi anyamata. Koma m’masomphenya ochokera kwa Ambuye, anamuuzza iye, “Koma inu mudzakhala ndi mwana wamkazi ameneyo.”

¹⁴ Ndipo iye anati ali ndi mtsikana wamng’onoyo pano usikuuno. Ine sindikudziwa, munthuyo akhoza... akhoza—akhoza kukhala mwa omvetsera, kapena mu—munthu

amene ine ndikumukamba? Kwinakwake? Ine sindikudziwa, winawake anangondiiza ine za izo, kunjako. O, ndi uyu mwana wakhala kumbuyo uko mommuno, wakhala kunja uko. Ndizo zabwino. Ndizo zabwino kwambiri. Kamunthu kakang'ono kokoma bwanji. Sizinali kutali kwambiri kuti ndiyende pa aliyense, ndi wokongola kwambiri, mwana wamng'ono, Ine ndikanati ndimulore iye abwere kuno ndi kudzapereka umboni. Mwinamwake iye atero pofika mawa, kapena nthawi ina pamene ife tidzakhala ndi misonkhano yathu.

¹⁵ Tsopano, mawa mmawa ndi Kadzutsa wa Amuna Amalonda. Kodi inu mwalengeza izo? Ine ndikuganiza, ndizo zonse. . . Ndi zabwino.

¹⁶ Ndipo tsopano tiyeni tikhale ndi laling'ono—phunziro laling'ono pa machiritso Auzimu. Ndi angati amakhulupirira mwa iwo? O, mai, ukhala usiku waukulu, pamene inu mukhale ndi chikhulupiriro monga chocho. Anthu amene amakhulupirira izo, ndizo zomwe zimatengera. Ndi za okhulupirira.

¹⁷ Tsopano, ndiye, ine ndinadzipezera pensulo ndi kuyamba kulemba mutu wina ndi zina zotero, ndipo. . . ndipo kenako Billy anagodga pa chitseko anati, “Adadi?”

¹⁸ Ine ndinati, “Dikira kanthawi pang'ono, ine sindinamalizebe izo.”

¹⁹ Iye anati, “Koma, M'bale Jack akukudikirani inu.” Kotero, ine—ine ndinayenera kubwera. Ine ndinamata, ndinalibe kopanira mapepala, Ine ndinapeza imodzi ya ma “johnny pini” a Meda kapena mtundu wina wa pini pano womwe iye ankautcha “bobby pini.” Ndi chomwe iyo inali, “bobby pini,” mtundu wina wa pini. Ndipo—ndipo ine sindimadziwa zochuluka za zinthu zimenezo, inu mukudziwa, ndipo ine ndinangoyiwona iyo ili pamenepo. Kotero, tsopano kupanga kopanira mapepala apa, kuti ndilekanitse chimene ine ndinali. . . ndinali ndi zolemba zina za mmawa; nkuzilekanitsa izo, china kwa chimzake.

²⁰ Ndipo pamene ine ndikukalamba. . . izo zinkakhala kuti ine ndinkakhoza basi kuwakumbukira Malemba amenewo ndi zinthu mophweka basi. Koma, inu mukudziwa, zimakhala zovuta kuti ndizichite. Kodi inu mukumalipeza vuto limenero, M'bale Jack, panobe? Ndiko kulondola, eya. Ine ndinamuuza M'bale Jack, kuno osati kale kwambiri, ine ndinati, “Inu mukudziwa, M'bale Jack,” ine ndinati, “Ine ndikufika pakuti ine sindikutha kukumbukira.” Ine ndinati, “Ine ndimayamba kunena chinachake, ndipo ine ndimayenera kudikira kaye.”

Iye anati, “Kodi—kodi pamenepo ndi patali pomwe inu muli?”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, kumeneko si kutali mokwanira?”

21 Iye anati, “Ayi.” Anati, “Ine ndimamuyimbira winawake pafoni ndi kuti ‘Kodi ukufuna chiyani?’” Ine ndimaganiza kuti inu mumandinamiza ine pamenepo, M’bale Jack, ine ndinapeza kuti izo nzoona kwambiri.

22 Inde, bwana. Mai, momwe inu mumayiwalira. Koma tiyeni ife tichite ntchito zathu zonse moyenera, chifukwa izo ziri mu bukhu, zojambulidwa zomwe ziti zidzaseweredwe pa tsiku lachiweruzo.

23 Tsopano, ife tiri ngati banja limodzi lalikulu. Ndipo ine sindikuganiza kuti ife talumikizidwa usikuuno, kudutsa dzikoli, monga ine ndimalalikirira uthenga wanga usiku wathawu. Ine ndikuganiza kuti mwina ndi mpingo wakudera kuno wokha. Koteru, usiku watha, ine ndithudi ndikuyamikira ulemu wanu woyimirira. . . Ine sindiyesere. . . Ine sindinayesere kutengerapo mwayi kwa M’bale Jack. Koma iye amandiuza ine nthawi zonse, “Nenani chomwe inu mukufuna kunena.” Ndipo koteru ine ndinangobwera pa nsanja ndipo ndinalalikira kachiphunzitso kakang’ono. Koma, koteru basi ife. . . ngati ena a abale anga achipembedzo.

24 Ine ndinali ndi loto, mmawa wina. Ine sindimalota nthawi zambiri, ine sindine wolota. Koma ine—ine ndinalota kuti ine ndinawona munthu, mnyamata wamng’ono atavala unyolo, ndipo iye amayesera kuti atulukemo, ndipo—ndipo ine ndinati. . . Winawake anandiuza ine, anati, “Amenewo ndi anthu owopsa, usati ukhale ndi chirichonse chochita ndi iwo.”

25 Ndipo ine ndinamuwona mnyamata wamng’ono uyu akutuluka mu unyolo wake koteru ine ndinangomusiya iye yekha. Ine ndinaganiza, “Ine ndingowona zomwe iye atachite.” Koteru pamene iye anatuluka kunjira, iye anali munthu wabwino. Ndipo ine ndinawawona ena akuyesera kuti atuluke.

26 Tsopano, ili ndi loto chabe. Ndipo ine ndinayenda chaku njira iyi ndipo ine ndinawona m’ba—m’bale, Roy Borders, bwenzi labwino kwambiri la ine, amakhala ku California. Zimawoneka ngati pali chinachake cholakwika, maso ake anali otsekedwa mwatheka, ndi aakulu kwambiri. . . mwina khansa kapena chinachake chinali pa maso ake. Ndipo ine. . . winawake ankayesera kundichotsa ine kwa iye. Ine ndinakuwa, “M’bale Borders! Mu Dzina la Ambuye Yesu, tulukani mu zimenezo!”

27 Ndipo iye samatha nkomwe kuyankhula, akunena, “M’bale Branham, izo zikuyenera kutengera chinachake choposa ichi. Ine basi sindingathe kuzigwira izo, M’bale Branham. Ine basi sindingathe kuzigwira izo.”

28 Ine ndinati, “O M’bale Borders.” Ine ndimamukonda iye.

29 Ndipo winawake anandikokera ine kutali, ndipo ine ndinayang’ana, ndipo anali dona atayima apa yemwe ine, pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono, ine—ine ndinkanyamula zogulagula kuchokera ku golosale kupita kwa

anthu. Ndipo dzina lawo linali Mayi Fenton, iwo akukhalabe mu Jeffersonville panobe, mzanga weniweni kwa mkazanga ndi ine.

³⁰ Ndipo iye anati, “M’bale Branham, tipulumutseni ife ku izi.” Anati, “Iyi ndi nyumba ya gehena.” Ndipo anati, “Inu simunamvetsetsedwe.” Ndipo anati, “Awa...Ndipo inu—inu simunawamvetse anthu awa, nawonso.” Anati, “Awa ndi anthu abwino, koma...” Ndipo ine ndinayang’ana cha kumeneko, ndipo ngati chipinda chapansi chachikulu, kapena—kapena makoma aakulu, pansu pa mphanga yaikulu; ndi simbi zachitsulo zazikulu, zokhuthala mainchesi eyiti kapena teni. Ndipo anthu, atasokonekera mmalingaliro mwawo, mikonu yopindika ndi miyendo, akumenyetsa mitu yawo monga *choncho*. Ndipo iye ankalira, akuti, “Apulumutseni anthuwa, M’bale Branham.” Anati—anati, “Tithandizeni ife, ife tiri mmavuto.” Iye iyemwini, ine ndikumudziwa iye, iye ndi wa...Ine ndikukhulupirira mpingo wa Khristu, kapena mpingo wa Chikhristu, wotchedwa Mpingo wa Abale. Kotero iye. . .

³¹ Ine ndinayang’ana pozungulira, ndipo ine ndinati, “Ine ndikanakonda ndikanatero.” Ndipo ndinapitirira kuyang’ana pozungulira; ndipo ine...langa laling’ono, thupi lochepa kwambiri ndi—ndi izo zazikulu, nsimbi zachitsulo zazikulu zimenezo; ndi anthu osauka awo mmenemo. Ndipo iwe sukanatha kuwafikira iwo, simbi zachitsulo zimenezo zinali ziri moyandikana pamodzi. Ndipo ine ndinayang’ana, ndipo iwo ankamenyetsa mitu yawo ngati kuti anali atasokonekera m’malingaliro awo.

³² Ndipo ine ndinawona magetsi ena akuthwanima cha kumeneko. Ndipo ndinayang’ana mmwamba, ndipo apo panayima Ambuye Yesu ndi zo—zo—zounikira za utawaleza pomuzinga Iye. Iye amayang’ana molunjika kwa ine, anati, “Apulumutse anthu amenewo.” Ndipo Iye anachokapo.

³³ Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, ine ndingawapulumutse bwanji iwo? Ine—ine ndiribe mphamvu zokwanira mmanja mwanga kuti ndithyole nsimbi zimenezo.”

³⁴ Kotero ine ndinati, “Nyumba ya gehena, perekana njira ku Dzina la Yesu Khristu.”

³⁵ Ndipo kulira konse ndi kuphulika, ndi—ndi miyala ikugudubuzika, ndi—ndi simbi zikugwa; ndipo anthu akuthamanga, akukuwa, “Tapulumutsidwa!” ndipo akufuula pamwamba pa liwu lawo, ndipo onse anapulumutsidwa.

³⁶ Ndipo ine ndinali kukuwa pamenepo “M’bale Roy Borders, inu muli kuti? Inu muli kuti? Mulungu akupulumutsa anthu Ake! Inu muli kuti, M’bale Borders?” Ine ndinadabwa nazo zimenezo.

³⁷ Inu mukudziwa, M’bale Borders ndi wamantha kwambiri. Inu mukuwudziwa uneneriwo, nonse...ambiri a inu mukutero,

inu mutenge matepi ndi zina zotero, zokhudza Kumadzulo kwa Gombe.

³⁸ Pali amuna akhala pomwe pano, usikuuno, omwe anali pamene pamene zimenezo zinkachitika, pamene ife tinayima pamene, pa ulendo wokusaka. Ndipo mtumiki yemwe anali kumvetsera usiku wathawu, ndi diso lochititsidwa khungu, iye anangobwera apo ndipo iye anati . . . anadzifotokoza yekha. Iye anali atavala magalasi a mtundu, pamwamba pa phiri. Iye anati, “M’bale Branham,” anati, “Ndine M’bale McHughes.” Iye anati, “Ine—ine ndinathandizira kuthandiza umodzi wa misonkhano yanu kamodzi, mu California.”

³⁹ Ine ndinati, “Ndine wokondwa kukudziwani inu, M’bale McHughes.”

⁴⁰ Kotero apo panali pafupifupi amuna twente atayima pamene. Ife tinali kunja kokasaka nguluwe za javelina. Ndipo ine ndinati, tsiku limene ndinali ndisanakwere phirilo, ine ndinati kwa M’bale Banks Wood, nonse a inu mukumudziwa iye, bwenzi langa, Ine ndinati, “M’bale Wood,” anatola mwala ndipo anawuponya m’mwamba, ndipo iwo unatsika pansu, ndipo ine ndinati, “PAKUTI ATERO AMBUYE, chinachake chikukonzekera kuti chichitike.”

⁴¹ Kotero, iye anati, “Ndi chiyani icho, M’bale Branham?”

⁴² Ine ndinati, “Ine sindikudziwa, koma mkati mwa maora twente foro inu mudzawona. Chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Ndicho chizindikiro chachikulu.”

⁴³ Ndipo tsiku lotsatira . . . amenewo anali madzulo ena. Tsiku lotsatira, pafupifupi 10 koloko, ife tinkakonzekera kutuluka. Aliyense anali ndi nguluwe zawo za javelina, ndipo ife tinali titayima pamene. Ndipo M’bale Mc Anally, inu mukudziwa, ndi onse a iwo, anali akuzikonza izo, ndipo—ndipo M’bale Borders ndi ine; ndi M’bale Roy Roberson, msirikali wopuma wolumala, wokondedwa kwambiri, mzanga wofunika wa ine, ndipo iye anali atayima pamene. Ndipo ine ndinayang’ana mmwamba, ndipo M’bale McHughes anati, “M’bale Branham, kodi Mngelo wa Ambuye amawonekera kwa inu pamene inu muli pa maulendo okasaka awa?”

⁴⁴ Ine ndinati, “M’bale McHughes, inde. Ndiko kulondola. Koma, ine ndinabwera kuno kuti ndidzachte ngati ndapumako.”

⁴⁵ Iye anati, “Chabwino, M’bale Branham,” anati, “Ine sindimatanthauza kuti ndikusokonezeni inu.”

⁴⁶ Ine ndinati, “Inu simunandisokoneze ine.”

⁴⁷ Ndipo ine ndinangoyang’ana pozungulira, ndipo ine ndinawona dokotala akuyang’ana pa diso lake. Tsopano, ine sindimamudziwa iye, iye anali atavala magalasi akuda, kumene ndi kowala moyipa ndi kwadzuwa ku Arizona. Ndipo ine

ndinayang'ana pa ilo, ndipo ndinamuona dokotala akumuuya iye, kuti, “Bwana, ine ndakhala ndikusamalira diso limenero kwa zaka, zaka ziwiri, chinachake monga chimenecho.” Anati, “Chiwengo chomwe muli nacho mu diso lanu, inu mudzataya diso lanu. Chikudya kubwerera mu kuwona kwanu, ndipo palibe njira yomwe ine ndingaziimitsire izo.”

⁴⁸ Ndipo ine ndinati, “Chimene iwe unandifunsira ine, ndi chifukwa cha diso lako. Magalasi adzuwa awo ndi chifukwa chakuti iwe uli ndi diso lowonongeka.”

⁴⁹ Iye anati, “Ndiko kulondola.”

⁵⁰ Ine ndinati, “Dokotala wako,” (ndinamufotozoza iye) “iye anakuuza iwe, masiku angapo apitawo, kuti ‘Iwe ulitaya diso limenero chifukwa—chiwengocho chikudya kuwona kwa disolo.’ Ndipo iye wakhala akulisamalira ilo kwa zaka zingapo, ndipo iye sangakhoze kuziimitsa izo.”

⁵¹ Iye anati, “M'bale Branham, izo ndi zoon.”

⁵² Ndipo ine ndinayamba kutembenuka ndi kuyang'ana, ndipo ine ndinawona mka—mkazi wamkulu kwambiri kuposa iye, wooneka ngati wakuda. Iwo amachokera kwinkwake kuno ku Arkansas. Ndipo kotero iye anakwezera mmwamba yake—yake—siketi yake nawonetsa mwendo wake kwa mwana wake, ndipo iye anati, “Mwana, iwe ukamuwona M'bale Branham, umuwuze iye kuti apempherere mapazi anga.” Ndipo anali ndi zotupa zazitali zikulendewera pakati pa zala zake ndi zinthu.

⁵³ Ine ndinati, “Amayi ako ndi mzimayi wa mutu wa imvi, ndipo iye anakweza mmwamba siketi yake, nakokera mmbuyo ake—masitonkeni ake ndipo anakuwonetsa iwe mapazi awo, ndipo anati iwe ukandiwona ine undiuzze kuti ndiwapempherere iwo.”

⁵⁴ Ndipo iye anati, “O, chifundo.”

⁵⁵ Ine ndinayang'ana mmbuyo ndipo ine ndinamuwona iye atayima pamenepo wopanda magalasi, masomphenya, Ine ndinati “PAKUTI ATERO AMBUYE, Mulungu wachiza diso lako, ndipo wawachiza amayi ako, nawonso.”

⁵⁶ Chapanthawi imeneyo, ine ndinatembenuka...Tsopano, panali mwamuna wakhala apa, anali atayima pamenepo. Ine ndinanena kwa M'bale Roy Borders...kapena M'bale Roy Roberson, anaika dzanja langa pa phewa lake, pakuti iye ndi msirikali wakalekale, Ine ndinati, “M'bale Roy, khalani pansu pa chinachake, mwamsanga ndithu, chinachake chikukonzekera kuti chichitike.”

⁵⁷ Iye anati, “Kodi inu mukutanthauza chiyani, M'bale Branham?”

⁵⁸ Ine ndinati, “Usayankhule! Lowa pansu pa chinachake, mwamsanga!” Ndipo ine ndinatembenuka ndi kunyamula fosholo, apo pambali pa malowo, ndipo ndinachoka kwa iwo

chifukwa ine ndinadziwa kuti izo zikanabwera pamene ine ndinali.

⁵⁹ Pambali pomwe pa chigwa chachikulu, kutalika ka eyiti kapena teni kuposa nyumba iyi, ndi “bokosi” la chigwa; monga moto unatsika kuchokera Kumwamba, ngati kamvuvulu, mapazi pang’ono chabe pamwamba pa pamene ine ndinayimapo. Ndipo anang’amba miyala kuchoka mphirimo, anapita kunja ndi kukadula nsonga za mitengo ya mkungudza, kwa mayadi handiredi kunja. Aliyense akuthamanga, akuyesera kulowa pansi pa magalimoto ndi china chirichonse. Iwo unabwerera mmwamba kachiwiri ndipo anawomba ngati bingu lalikulu. Unabwerera kupyola m’mlengalenga kachiwiri, ndi kubwera pansi kachiwiri. Iwo unachita izo katatu. Ndipo pamene izo zonse zinatha, iwo anabwera ndipo anafunsa, “Kodi izo zimatanthauza chiyani?”

⁶⁰ Ine ndinati, “Ine sindikufuna kukuuzani inu; icho chinali chizindikiro cha chiweruzo. Mmasiku ochepa, chivomerezi chachikulu chidzakantha Kumadzulo. Ndipo icho sichiyima. California, Los Angeles adzamira. Iye akupita pansi. Iye adzatsetserokera momwe m’nyanja.” Ndipo masiku awiri zitachitika zimenezo, chivomerezi cha ku Alaska chinagwedeza Alaska.

⁶¹ Ndipo kenako, msonkhano wotsiriza umene ine ndinali nawo ku California, ndikuyankhula, ndipo ine sindinadziwe palibe chinachitika mpaka ine nditafika pa msewu, Izo zinamuza California, anati—anati, “Kapernao, Kapernao, mzinda umene umatchedwa ndi dzina la angelo,” (ameneyo ndi Los Angeles) “wadzikweza wekha mmwamba, koma udzatsitsidwa pansi kugehena. Pakuti ngati ntchito za mphamvu zinachitidwa mu Sodomu zimene zachitidwa mwa iwe, iye akanakhala akuyimabe mpaka lero.”

⁶² Tsopano, masiku angapo apitawa, kubangula kwakukulu ndi kuphulika. Ndiye, apa pakubwerapo pepala la sayansi, linati, “Zonse ndi zisa za uchi, akuyenera kulowa pansi.” Iwo akuzidziwa basi izo.

⁶³ Ndipo inu tawonani, madzi adzabwerera mpaka komwe ku Nyanja ya Salton. Los Angeles wawonongekera ku chiweruzo. Ine ndikukuuzani inu izo zisanachitike, kuti inu mudziwe pamene izo zizidzachitika. Ine sindinayankhulepo zimenezo pandekha. Ndipo ine sindinayambe ndakhalapo ndi Iye kuti andiuze ine chinthu chimodzi kupatula chimene chinachitika. Ndipo inu mukhoza kuchitira umboni za zimenezo. Uko nkulondola. Liti? Ine sindikudziwa.

⁶⁴ Ine ndinatuluka kunja, ndipo iwo anandiuza ine zomwe ine ndinanena. Ndipo ine ndinamvetsera, ndinabwerera ndi kukafufuza Lemba. Inu mukudziwa, Yesu anati, pafupifupi mu mawu omwewo, zokhudza Kapernao; ndipo Sodomu ndi

Gomora anali—anali pansu pa Nyanja Yakufa, ine ndikuganiza panali pamenepo. Ndipo kenako, pafupifupi zaka handiredi patsogolo pake, Kapernao anatsetserekerera m'nyanja, ndipo ali mu nyanja. Mulungu yemweyo amene anamuyika Sodomu m'nyanja chifukwa cha machimo ake, Mulungu yemweyo amene anamuyika Kapernao m'nyanja chifukwa cha machimo ake, Mulungu yemweyo adzamuyika Los Angeles mu nyanja chifukwa cha tchimo lake, mzinda umenewo wa—wa chibvundi.

⁶⁵ M'bale Roy Borders akuchita mantha mpaka ku imfa. Ine sindikudziwa kaya kuti... zomwe izo zinkatanthauza, izo, kapena chiyani, ine sindikudziwa.

Tiyeni ife tipemphere.

⁶⁶ Ambuye, ndi kwabwino kuti tichitire umboni kwa omvera enieni. Ife tikukhulupirira, Ambuye, thandizani kusakhulupirira kwathu. Ndipo ife tikuzindikira kuti tikupita mmusi momwe tsopano ku mapeto a dziko. Basi ndi nthawi yanji, ife sitikudziwa. Koma chinsinsi chimenecho cha kutengedwa kwa Mkwatibwi; limodzi la masiku awa, Ambuye, ife tidzakhala—ife tidzakwatulidwa, kutengedwera mmwamba ndi Iye. Ndipo ife tikuyembekezera tsiku limenero. Konzekeretsani mitima yathu, Ambuye.

⁶⁷ Alipo ambiri, ife tikuyang'ana, agona apa pa zikuku ndi machira awa, amuna ndi akazi amene ali omangidwa ndi mdani. Pali anthu akhala kunjira uko, mwinamwake, ngati Inu simuwakhudza iwo, iwo afa ndi matenda a mtima. Mwina ena a iwo adyedwa ndi khansa.

⁶⁸ Ndipo Atate, Inu mukudziwa mtima wa munthu aliyense. Inu mukudziwa ngati izo ziri zowona kapena sizowona. Ndipo ife tikunena zinthu izi chifukwa kuti ife tikudziwa chimene Inu mwachita, mphamvu Yanu yaikulu yapulumutsa ambiri. Ndife mboni za izo, ngakhale iwo amayesa kuti atiwuze ife kuti “zinthu zimenezo sizimachitika.” Koma izo zimatero, Ambuye. Ife ndife mboni.

⁶⁹ Ine ndikupemphera usikuuno, Ambuye, kuti mwinamwake Inu muwumba chikhulupiriro mmitima ya anthu awa, kuti aliyense wa iwo amasulidwa, odwala onse awa ndi anthu osautsika. Mulole izo zikhale zophweka kwambiri, Ambuye, mungotilora ife, pamene ife tikuyesera kuti tiphunzitse Mawu. Mulole Mzimu Woyera utenge zolakwitsa zanga, Ambuye, ndi kuzikonza izo mmitima ya anthu. Ndipo muwupange iwo kukhala weniweni, usiku weniweni kuti...kuti Iye akhoza kudzikhazika Yekha mu mtima wa wokhulupirira aliyense pano. Ife tawuyika usiku uno kwa cholinga chimenecho, Ambuye. Mulole iwo amene sanapulumsidwe, pamwamba pa zinthu zonse, akhale okonzeka; akonzekere tsopano, pamene zitseko za chifundo zikadali zotseguka. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

70 Tsopano ife titembenezira ku Malemba, kuti tiyambirepo, ndipo mu . . .

71 Wina anaika cho—cholemba apa pa desiki, ndipo anati iwo “anatolera chopereka” cha ine usikuuno. Izo sizinali zofunikira, musati muzichita zimenezo. Ine sindingathe kuchibwezanso. Ine ndikukumbukira nthawi ina, Calgary, Canada, ife tinatolera . . . chopereka ichi chinatoleredwa. M’bale Jack ankayesera kundiuza ine . . . Mkazi wanga atakhala kumbuyo uko; iye, ana anali ndi zipinda ziwiri zakale zomwe ife tinkakhalamo, iye ankayenera kuyika bulangete pakhomo kuti asunge chi—chitseko chotsekedwa kuti ana asatenge chibayo. Ndipo iye anati . . . Iye anati kwa ine, “M’bale Branham, izo si zabwino kumuchitira iye mwanjira imeneyo.” Kotero, inu mukukumbukira chochitikacho. Iwo anatenga, ine ndayiwala kuti anali masauzande a madola angati.

72 Ndipo ine ndinati, “O, kazibwezeni izo, M’bale Jack.”

73 Iye anati, “Tsopano, ife tichita motani izo?” Kotero, ine ndinagula malowo ndipo ali pamenepo. Chotero, kwa ulemerero ndi ulemu wa Mulungu. Ife tinawasunga iwo kwa zaka zingapo, mkazanga ndi ine, ngati mphatso yochokera ku mpingo, anthu.

74 Ndipo kenako ine ndinaganiza, “Izo sizikumveka bwino. Ine sindinabweretse kalikonse mdziko lino, ndi zotsimikizika kuti ine sindidzatulutsamo kalikonse.” Kotero ine ndinapotoloka ndipo ndinawagawa iwo, ndipo ndinawapereka iwo kubwerera ku kachisi. Kuti pamene ine ndamaliza, bwanji, wantchito wina wa Mulungu, ngati kuli mawa, adzawagwiritsa ntchito iwo ndiye. Mukuwona? Kotero, zikomo inu mokoma kwambiri, abwenzi. Mulungu akudalitseni inu, chifukwa cha izo.

75 Tsopano, mu Yakobo, Bukhu la Yakobo, mutu wa 2, ife tikufuna kuti tiwerenge, kuyambira pa ndime ya 21.

76 Ndipo tsopano, ine basi pafupifupi . . . Kanthawi pang’ono kuti kuphunzitsa, ndipo kenako ife tiyamba kupempherera odwala mwamsanga momwe ife tingathere, ndi kuwatengera anthu ochuluka basi kudutsa mu mzere wa pemphero uwu momwe ife tingathere. Ndipo tiyeni, komanso, tizikumbukira ndiponso . . . Ine sindikufuna kuti ndimuyiwale Mlongo Anna Jeanne ndi M’bale Don, ndi iwo, Ine ndikuganiza iwo ali mu Thailand kwina kwake. Sichoncho iwo? Kupita kuti? Bangkok, ndi—ndi munda ya umishonale. Pali zinthu zambiri zomwe inu mumaziganizira masana, inu mumafuna kuzinena pamaso pa anthu. Ndiye pamene inu mubwera pano, inu—inu simumakhoza kuganiza za izo, inu mumachulukidwa pansu pomwe pa phunziro limenero.

77 Ndipo tsopano, mu Yakobo apa, mutu wa 2. Ndipo ife tikuti tiyambire ndi ndime ya 21 ya mutu wa 2 wa Yakobo Woyera, ndi kuwerenga ga—gawo la Iwo. Ndime ya 21 ya mutu wa 2.

Kodi Abrahamu atate wathu sanayeseḁwe wolungama ndi ntchito, pamene iye anampereka Isake mwana wake nsembe pa . . . guwa?

Tawonani inu momwe chikhulupiriro chinagwirira ntchito pamodzi ndi ntchito zake . . . chikhulupiriro chinapangidwa kukhala changwiro?

Ndipo lemba linakwaniritsidwa limene limanena, Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo izo zinawerengeredwa kwa iye chilungamo: ndipo iye anatchedwa Bwenzi la Mulungu.

⁷⁸ Tsopano, phunziro langa usikuuno . . . Ndipo gwirani ma Baibulo anu tsopano, chifukwa ine ndiri nawo Malemba ambiri ndawalemba apa. Ngati ife sititenga nthawi yayitali, ine ndilozera kwa ambiri a iwo. Phunziro langa ndi: *Ntchito Ndi Chikhulupiriro Chofotokozedwa*. Tsopano, kumbukirani: *Ntchito Ndi Chikhulupiriro Chofotokozedwa*. Ntchito zimasonyeza kuti chikhulupiriro chagwira kale, mwawona. Mukuwona? Tsopano, ife timasankha izi chifukwa ife . . . Ine ndikukhulupirira kuti izo zingatithandize ife kuti timvetse. Tsopano mvetserani mwacheru kwenikweni, ndipo ife tilowa mu izo monga phunziro la Sande Sukulu.

⁷⁹ Apa Yakobo akufotokoza mu chiphunzitso chake, kuchokera pa Genesis 22:1-9, chimene *munthu* ankachiwona mwa Abrahamu.

⁸⁰ Tiyeni tingobwerera mmbuyo, ine ndiri ndi Malemba ngati ndawalemba apa. Mu Genesis, mutu wa 22, ndi ndime ya 1 mpaka ya 9.

Ndipo kunali zitapita zinthu izi, kuti Mulungu anamuyesa Abrahamu, ndipo anati kwa iye, Abramamu . . . Abrahamu: ndipo iye anati, Tawonani, ndine pano.

Ndipo iye anati, Tengatu mwana wako, wana wako mmodzi yekhayo, Isake, amene iwe umkonda, ndipo upite ku dziko la Moriya; ndi kukampereka iye . . . ikhale nsembe yopsereza pa limodzi la mapiri limene Ine ndidzakuuza iwe.

Mwawona, Iye sanamuuze iye nkomwe lomwe ilo inali. Inu muzingopitirira pamene Mulungu ayankhula, inu muzipitirira kuyenda. Mukuwona?

Ndipo Abrahamu analawirira m'mawa, namanga chishalo pa buru, ndipo anatenga awiri a anyamata ake pamodzi naye, ndi Isake mwana wake, namangirira nkhu ni za nsembe yopsereza, ndipo ananyamuka, ndipo anapita ku malowo . . . amene Mulungu anamuza iye za iwo . . . anamuza iye.

Ndipo pa tsiku lachitatu Abrahamu anatumula maso ake, ndipo anawona malowo patali.

Ndipo Abrahamu anati kwa anyamatawo, Khalani inu pano ndi buluyu; ndipo ine ndi mwanayu tipita kutsidyako ndi kukapembedza, ndi kubweranso kwa inu.

⁸¹ Tsopano, iye anali nazo mmalingaliro ake tsopano, iye akupita kuti akamuphe mwana wake wamwamuna, chifukwa Mulungu anamuuzza iye kutero. Koma yang'anani pa Lemba apa.

...Ine ndi mwanayu tidzapita kutsidyako ndi kukapembedza, ndi kubweranso kwa inu. (Iye ndi mwanayo.)

Ndipo Abrahamu anatenga nkhuni ndi nsembe yopsereza, ndipo anaziika izo pa Isake mwana wake; ndipo iye anatenga moto m'dzanja lake, ndi mpeni; ndipo iwo onse awiri anapita... iwo pamodzi.

Ndipo Isaki ananena kwa Abrahamu atate wake, ndipo anati, Atate wanga: ndipo iye anati, Ndine pano, mwana wanga. Ndipo iye anati, Tawonani moto ndi nkhuni: koma alikuti mwanawankhosa wa nsembe-yopsereza?

Ndipo Abrahamu anati, Mwana wanga, Mulungu adzadzifunira yekha mwanawankhosa wa nsembe yopsereza: kotero iwo anapita onse awiri pamodzi.

Ndipo iwo anafika ku malo kumene Mulungu... anamuuzza iye za iwo; ndipo Abrahamu anamanga pamenepo guwa la nsembe, anakonza nkhuni, anamumanga mwana wake wamwamuna... Isake mwana wake, ndipo anamugoneka iye pa guwa la nsembe pa nkhuni.

Ndipo Abrahamu anatambasula dzanja lake, ndipo anatenga mpeni kuti amuphe mwana wake.

Ndipo mngelo wa AMBUYE anamuitana iye kuchokera kumwamba, ndipo anati, Abrahamu, Abrahamu: ndipo iye anati, Ndine pano.

Ndipo iye anati, Usaike dzanja lako pa mwanayo, kapena usamchitire iye kanthu: pakuti tsopano Ine ndadziwa kuti iwe umawopa Mulungu, poona kuti iwe sunandikaniza mwana wako, wako...kwa ine... mwana wako mmodzi yekhayo kwa ine. (Ndi ntchito yotani!)

⁸² Tsopano, ife tikupeza apa kuti Yakobo akumulungamitsa Abrahamu ndi *ntchito* zake.

⁸³ Koma tsopano, mwa Paulo, mu Aroma, Bukhu la Aroma, wa 8... mutu wa 4, 4:1 mpaka 8. Ine sindiwerenga iwo wonse, koma ndingowerenga gawo la iwo.

Ndipo *ife tidzati chiyani ndiye kuti Abrahamu atate wathu, mwa thupi, anapeza?*

Pakuti ngati Abrahamu analungamitsidwa . . . (Inu mukukumbukira, ife tinatenga mawu usiku watha, “kulungamitsidwa.”) . . . mwa ntchito, ali nako kudzitamandira; koma osati pamaso pa Mulungu.

Pakuti lemba linena chiyani? Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo zinawerengeredwa kwa iye chifukwa cha chilungamo.

Ndipo kwa iye amene agwira ntchito, mphotho siimawerengedwa chisomo, koma ngongole.

⁸⁴ Tsopano—tsopano chimene Paulo akulozera apa, ndi chimene *Mulungu* anachiwona mwa Abrahamu.

⁸⁵ Tsopano tiyeni . . . ngati inu . . . ngati ife sitinatembenezire mochuluka kwambiri, ife tikanabwereranso ku Genesis, mutu wa 15, ndi ndime ya 6; 15:6, ine ndikukhulupirira ndi zolondola. Ife tiyambira pa 5.

Ndipo iye anamtulutsa iye kunjja, ndipo anati, Yang'anatu tsopano molunjika kumwamba, ndipo uwuze nyenyezi, ngati iwe uli wokhoza kuziwerenga izo: ndipo iye anati kwa iye, Momwemonso idzakhala mbewu yako.

Ndipo iye anakhulupirira mwa AMBUYE; ndipo iye anawerengera izo kwa iye chilungamo.

⁸⁶ Tsopano amuna awiri amene ankayankhula pa chikhulupiriro: Paulo anamulungamitsa Abrahamu ndi zimene *Mulungu* anawona mwa Abrahamu; koma Yakobo anamulungamitsa Abrahamu ndi chimene *munthu* anachiwona mwa—mwa Abrahamu.

⁸⁷ Mwawona, tsopano, Yakobo anati, “Iye amalungamitsidwa ndi ntchito zake.”

⁸⁸ Paulo anati, “Iye analungamitsidwa ndi chikhulupiriro.”

⁸⁹ Koma mukuwona, Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndicho chimene *Mulungu* anachiwona mwa iye; iye anakhulupirira Izo. Komano kenako pamene iye anayamba kuchita ngati kuti izo zinali zitachitika kale, ndicho chimene *munthu* anachiwona mwa iye.

⁹⁰ Ndipo izo ndi chimodzimodzi monga izo ziliri kwa ife, chifukwa ntchito zathu zimafotokoza chikhulupiriro chimene ife tiri nacho. Koma ngati ife tikuwopa kuchita pa zomwe ife timazikhulupirira, ndiye ife sitimazikhulupirira Izo. Mwawona, inu mukuyenera kuti muzikhulupirira Izo.

⁹¹ Ntchito za Abrahamu zinali kufotokoza chikhulupiriro chimene iye anali nacho mmalonjezo a Mulungu. Tsopano, Abrahamu, kumbukirani, iye anali wausinkhu wa zaka nainte,

kapena, wausinkhu wa zaka handiredi, ndipo Sara anali wausinkhu wa zaka nainte. Ndipo tsopano iwo anali okalamba mu usinkhu, atapitirira pobereka ana, anakhala kwa zaka zambiri, zambiri. Ndipo iwo anali atakhala limodzi moga mwamuna ndi mkazi kuyambira iwo ali aang'ono, ndipo analibe ana. Komabe, Mulungu anamuuzza iye pamene iye anali usinkhu wa zaka sevente faivi ndipo Sara sikisite faivi, "Inu mudzakhala ndi mwana." Ndipo iye anakhulupirira lonjezo la Mulungu. Iye anakhulupirira Izo. Tsopano, mukuwona, iye anakonzekera chirichonse cha mwana ameneyu. Mwawona, ndicho chimene *Mulungu* anawona, pamene iye anakhulupirira Mulungu; ndipo *munthu* anawona zomwe iye anachita kuti afotokoze zomwe iye anakhulupirira. (Ndipo ndi chinthu chomwecho chimene chikugwira ntchito usikuuno, chimodzimodzi momwe izo ziliri ndi ife.) Izo zawululidwa kwa iye. Mwawona, izo zinali zitawululidwa kwa iye, kotero iye anazikhulupirira izo chomwecho, ndipo ankachita ngati kuti izo zinali zitachitika kale.

⁹² Tsopano, tiyeni tingoyima pamenepo, miniti yokha. Nthawi zina ife sitimamvetsetsa izi. Anthu amakhala otengeka, ndipo iwo amayesera kuchita pa kutengeka. Izo sizingagwire ntchito.

⁹³ Tsopano, ine ndiri ngati M'bale Hierholzer pano, ndife—ndife amuna achikulire, ndipo ife takhala mu . . . ichi nthawi yayitali, ndipo ife tawona zabwino ndi zoyipa, ndi—ndi chirichonse. Ndi kupempherera odwala, kuzungulira dziko lapansi, ndi kuwona zo—zokhumudwitsa za anthu, ndi kuwona ma—ma "Aleluya" kuchokera mbali iliyonse. Ndiye, zonsezi, ife timaphunzira nazo. Tsopano, pamene tiri anyamata aang'ono, pamene ife tinayamba kulalikira izi, M'bale Hierholzer, moga inu munkayamba kusambira. Chinthu choyamba, inu mukudziwa, zinkakhala kuti ine ndimatuluka, ndipo ine ndimkhoza. . . M'bale Jack, ine ndakhala naye M'bale Brown kuti azindiyendetsa ine pa msewu, usiku pambuyo pa usiku, kuti ndiyesere kudzipweretsa ndekha kwa inemwini. Ine ndimakhocha kuyima pamenepo, ngati kamwana kakang'ono, kumawaza madzi, ndikumawona masomphenya, inu mukudziwa. Ndipo ine ndimangokhala pamenepo mpaka M'bale Brown. . .

⁹⁴ Ine ndikukumbukira usiku wina, ine sindidzaiwala izo, uko ku San Jose kapena kwinakwake. Iye anabwera kuti adzandidzutsa ine, ine ndinali ndisanagone kwa masiku angapo ndipo ine sindimadziwa kuti ndimayankhula ndi bamboyo, koma anati ine ndinamuuzza iye. Ndinayamba kulira, ndinati, "Ine ndikupita kunyumba." Mukuwona?

⁹⁵ "Chifukwa," iye anati, "iwe sungathe kupita kunyumba. Kuli msonkhano ukuchitika kumunsi kumeneko."

⁹⁶ Ine ndinati, "Chabwino, ine ndikonzeke mu maminiti ochepa kuti ndizipita kunyumba." Mwawona, kupitirira basi, pambali

pa inemwini, pafupifupi. Mwawona, ine ndinali mnyamata pamenepo.

⁹⁷ Monga inu mukuphunzira kusambira, inu mukudziwa, inu mumawaza madzi ndi kumapita mowoloka dziwe, ndipo “huhhh, huhhh, huhhh, ine ndamupangitsa iye!” Tsopano, inu mutatha kuphunzira kusambira, kupalasa kumakhala kokoma kwambiri, ndipo iko “sikumakutopetsani inu” kwambiri. Mwawona, ndi zimenezotu, inu mumaphunzira momwe mungachitire izo; ndi kudula ngodya iliyonse ndikuzipanga izo bwinoko, ndipo izo ndizophwekerako. Mukuwona?

⁹⁸ Mnyamata wamng’ono yemwe sanayendepo, akhoza kuyesera kuyenda mkanjira aka apa, iye angakhoze kugwa ka dazeni ndi kukhala “wotoperatu” iye asanakafike uko. Koma aliyense amene amadziwa kuyenda, wothamanga, angathe kuyenda motsika kanjirako ndipo osazindikira nkomwe kuti akuchita izo. Chabwino, iye anali nazo izo kuyamba nkuyamba, ndi zomwe iye ali tsopano.

⁹⁹ Chabwino, ndizo chimodzimodzi ndi kulalikira machiritso Auzimu kapena china chirichonse. Pamene inu mukupita, inu mumayamba kuphunzira. Ngati inu simukuphunzira, pali chinachake cholakwika. Mwawona, inu mukuyenera kuphunzira, ndipo inu mukuyenera kuphunzira momwe mungamuvomerezere Mulungu ndi chimene izo zimatanthauza kwenikweni.

¹⁰⁰ Ife timazilola izo, nthawi zina timati, “Chabwino, munthu uyu analibe chikhulupiriro chokwanira, munthu uyu sanachite *izi* ndi *izi*.” Pali chifukwa pamenepo cha zimenezo, pali chifukwa. Nthawi zina ndi tchimo losalapidwa. Inu mukhoza kutsanulira galoni ya mafuta pa munthu, ndi kufuula mpaka inu mutasasa mawu, izo sizingamusunthe konse mdierekezi ameneyo. Ayi, bwana! Inu mukuyenera kuvomereza izo. Ndi zimene kuzindikira kumachita, kumati, “Pitani mukazikonze izo, kazitulutseni izo.”

¹⁰¹ Koma ndi zochedwa kwambiri kuchita zimenezo, inu mukuwona. Ndipo kenako—kenako ena onse amalephera kupirira, ndipo iwo amati, “Aa, ine sindinapemphereredwe konse.” Koma ife tikufuna kuti tipeze njira tsopano, imene... chimene chimachitika, maziko enieni a machiritso Auzimu.

¹⁰² Tsopano, mphatso, monga momwe ine ndinanenera usiku watha, “Mphatso ndi yodabwitsa, koma inu simungaike kokafikira kwanu Kwamuyaya pa mphatso.” Inu simungakhazikike pa chaching’ono, ndipo mpha—mphatso ndi yaing’ono. Ndipo Satana akhoza kutsanzira mphatso iliyonse yomwe Mulungu ali nayo, iye akhoza kupanga chinachake chimodzimodzi basi monga icho, mwawona, chimodzimodzi. Chotero, ife tiyenera kuziyang’ana izo.

103 Monga nthawi zina ine ndimafotokozerwa za kufuula; ine ndawonapo ziwanda zikufuula. Um-hum. Kuyankhula m'malirime, ine ndawonapo ziwanda zikuyankhula m'malirime. Zedi, iye amatsanzira Izo. Izo si zenizeni, koma izo zimatsanzira Izo, inu mwawona, amazipangitsa izo kuwoneka ngati ndi chenicheni. Ndipo anthu nthawi zina, omwe samadziwa kusiyana, amazinena *izi* kuti ndi “zenizeni” pamene izo siziri zenizeni.

104 Ndipo chinthu chomwecho chimene iwo amachita pa machiritso Auzimu. Iwo amaganiza, “Chabwino, ndi nkhabakamwa, kapena chinachake chonga icho.” Siziri choncho. Ndi chenicheni, chikhulupiriro chosapitsidwa mu zomwe Mulungu ananena kuti ndi Choonadi. Ndipo icho chimagwira! Ndipo pamene icho chakhazikika, palibe chomwe chingasunthe icho. Icho chikhala pamenepo. Ndipo koteru, kuyenda ngodya izi, . . .

105 Tsopano, *chikhulupiriro* ndi “vumbulutso lochokera kwa Mulungu.” Tsopano, chikhulupiriro ndi vumbulutso. Apo ndi pamene ine ndikufuna kuti ndikhale, pamenepo, mphindi chabe. Ndi vumbulutso. Iye waziwulula izo kwa inu mwa chisomo Chake. Si zimene inu munachita. Inu simunadzizwirire nokha ntchito mu chikhulupiriro. Inu mumakhala nacho chikhulupiriro, icho chimaperekedwa kwa inu mwa chisomo cha Mulungu. Ndipo Mulungu amaziwulula izo kwa inu, choncho chikhulupiriro ndi vumbulutso. Ndipo Mpingo wonse wa Mulungu wamangidwa pa vumbulutso.

106 Mtumiki wa Baptisti anandiuza ine, osati kale kwambiri, iye anati, “Ine sindingathe kuvomereza vumbulutso.”

107 Ine ndinati, “Ndiye iwe sungavomereze Baibulo. Inu simungakhoze kumulandira Khristu, chifukwa Iye ndi Vumbulutso la Mulungu. Iye ndi Mulungu wowululidwa mu thupi.” Choteru, Mpingo wonse wamangidwa pa vumbulutso Lauzimu.

108 Yesu anati kwa (Ine ndikukhulupirira anali Petro) . . . anati, Iye anati, “Kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu ndine ndani?”

109 Iye ankayankhula kwa ophunzira Ake. “Ndipo ena anati Inu ndinu ‘Eliya,’ ndi ‘Mose,’ kapena ‘Mmodzi wa aneneri,’ ndi ‘Yeremiya.’”

110 Iye anati, “Koma inu mumati ndi ndani?”

111 Iye anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.”

112 Tsopano, mpingo wa Roma Katolika umati, “Iye ankayankhula kwa Petro, ‘Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga.’”

113 Aprotostanti anati, “Iye ankaumanga Iwo pa Iyemwini.”

114 Tsopano, iwo akanakhoza kukhala olondola. Koma, kwa ine, onse a iwo akulakwitsa. Izo zinali pa vumbulutso lauzimu la Yemwe Iye anali. “Thupi ndi mwazi sizinaululire izi kwa iwe, Petro. Koma Atate Anga, omwe ali Kumwamba, awulula izi kwa iwe. Ndipo pa thanthwe ili,” vumbulutso la Yemwe Iye ali; pa vumbulutso: Iye ndi Mawu, mu chonsecho. “Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizingakhoze kuulaka Iwo.” Izo zinasonyeza kuti zipata za gehena zikanadzakhala zikulimbana Nawo.

115 Abele, mwa chikhulupiriro, vumbulutso, (panalibe Baibulo lolembedwa m’masiku amenewo), mwa . . . Abele, mwa chikhulupiriro, anapereka kwa Mulungu nsembe yopambana kuposa ija ya Kaini. Chimene Mulungu anachichitira umboni, “Iye anali wolungama.” Bwanji? Mwa chikhulupiriro. Motani? Mwa vumbulutso! Mwa vumbulutso, Abele anapereka kwa Mulungu nsembe yopambana kwambiri, chifukwa izo zinaululidwa kwa iye kuti sizinali zipatso za kumunda, iwo anali magazi.

116 Ndi chifukwa chake anthu ena akhoza kukhulupirira Izo, ndipo ena sangakhoze kuzikhulupirira Izo, ena amayesera kudzipangitsa kukhulupirira Izo.

117 Mu gulu la anthu, pamene mzere wa pemphero ukudutsa, inu mupeza ena . . . ndipo onse anali anthu abwino, ife titero. Alipo ena amene akuyesera zolimba kuti akhulupirire Izo, akuyesera kuti adzigwirire ntchito okha mu Izo. Ena sangathe basi kuchita izo nkomwe. Ndipo ena, ndi mwa chisomo basi, izo zimangoperekedwa kwa iwo. Tsopano, apo pali kusiyana. Mukuwona? Zimenezo zimachita izo. Ndilo vumbulutso lenileni, chifukwa chikhulupiriro ndi vumbulutso lochokera kwa Mulungu. Izo ziyenera kuwululidwa poyamba.

118 Yesu anafotokozera momveka bwino zimenezi pamene Iye anati, “Palibe munthu angakhoze kudza kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye poyamba, kapena atandiwululira Ine kwa iye poyamba.” Inu mukuyenera kuwerenga zimenezo. Ndi Yakobo Woyera, kapena, Yohane Woyera 6:44 ndi mpaka 46. Iwo sankadziwa Yemwe Iye anali. Iwo ankaganiza Iye anali munthu wamba chabe. Iwo ankaganiza kuti Iye anangokhala, monga anthu amachitira lero, mneneri wina. Iye anali mneneri, Iye anali Munthu wamba, koma panali choposa zimenezo.

119 Monga ngati usiku wathawu, ndikuyankhula . . . Pamene inu mupeza bukhulo, inu mudzawona mwinamwake chisokonezo pang’ono pamenepo pa zomwe ine ndinanena, “Mabuku awiri a Moyo.” Ilo ndi Bukhu lomwelo, koma limodzi la iwo ndi kubadwa kwanu kwachilengedwe, linalo ndi kubadwa kwanu kwauzimu. Wina amatsogolera kwa wina, monga phesi la tirigu. Chabwino, tsopano, inu mumanena za ine, inu mumayankhula za ine monga munthu wamoyo. Koma pali gawo la ine pano,

ndi munthu ameneyo, yemwe ayenera kuwonongeka. Ndilo Bukhu limene dzinalo likuchokerako. Koma Wamuyayayo, mmodzi Wokonzedweratuyo, mmodzi Wosankhidwayo, dzina silingakhoze konse kubwera kuchoka kumeneko chifukwa ilo nthawizonse linali pa Ilo. Ilo silingakhoze kuchotsedwa konse. Inu mudzaziwona izo mu bukhu, kotero kuti muchoke ku chisokonezo chanu. Mudzazipeza izo mwanjira imeneyo. Chifukwa, ine ndikuganiza, M'bale Vayle, yemwe anaika galamala yoyenera kwa ilo, anandikumbutsa ine za ilo lero. Ine ndinati, “Uko nkulondola.”

¹²⁰ Abaptisti amakhulupirira kuti pali mabuku awiri osiyana. Ndipo mwanjira ina ndi mabuku awiri osiyana, ndipo mwa njira ina si mabuku awiri osiyana. Ndine anthu awiri osiyana. . . Ndine thupi ndi moyo ndi mzimu, anthu atatu osiyana, koma ndine. . . chimodzi chokha chimandipanga kukhala munthu.

¹²¹ Pali Bukhu limodzi lokha la Moyo. Monga panali nyongolotsi imodzi ya—ya tirigu imene inatulukira kudzera mu phesi, ndipo inayenda kudutsa mu ngayaye, ndipo kudutsa umo m'mankhusu, ndi kulowa mu tirigu; njira yonse kumeneko, inu mukuti, “Tsopano, uyo ndi tirigu atagona pamenepo.” Iye si tirigu, ndi phesi, koma palimodzi ndi tirigu. Mwawona, ndi tirigu chifukwa zonsezo ndi phesi limodzi, koma tiriguyo ndi chimene inu mukuchikamba, njere pa mapeto pake. Zinazo zinali chonyamulira, izo zikuyenera kuwonongeka. Ndipo ndiwo amodzi—malo amodzi amamveka ngati inu mukhoza kupeza dzina lanu litachotsedwa mu Bukhu la Moyo la Mwanawankhosa, ndipo malo ena inu simungathe kuchita izo. Kotero, ndi pamene izo ziri. Izo zonse ziri mu vumbulutso lalikulu limenero uko, limene linapangidwa kudziwika mu nthawi ya Zisindikizo Seveni. Chifukwa chiyani izo ziri, momwe anthu ena sangakhulupirire Izo?

¹²² Yesu ananena kuti “Palibe munthu angabwere kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye poyamba. Ndipo onse amene Atate andipatsa Ine, adzabwera kwa Ine.” Palibe munthu angakhoze kumvetsa Yemwe Iye ali, kapena momwe Izo ziliri, pokhapokha izo zitawululidwa kwa inu mwa vumbulutso la Mulungu. Ndiyeno chikhulupiriro mu zimenezo, inu mumachita mogwirizana. Mukuwona? Apa ife tikuwona poyera kuti Mulungu amawululidwa mwa Yesu, ndipo okhawa amene anaikidwiratu kuti adzachiwone, adzachiwona icho. Onetsetsani kuti mwawerenga Lemba ili, ine ndinalidumpho ilo ndiye, la Yohane Woyera 6:44 mpaka 46. Ine ndinalisiya ilo chifukwa ine ndimaganza kuti mwina tikhala nayo. . . mwina palibe nthawi yokwanira kuti tidutsemo, chifukwa wotchi imeneyo kumtunda uko ikungopitirira kuyenda.

¹²³ Ndipo kotero ife. . . Inu mukuzindikira, “Palibe munthu, palibe munthu angakhoze kubwera pokhapokha Atate Anga atamukoka iye poyamba. Ndipo onse amene Atate andipatsa

Ine, iwo adzabwera.” Iwo adzachizindikira Ichu. Palibe munthu wina angakhoze kuchita izo, palibe munthu wina, ziribe kanthu wabwino bwanji, yemwe iwe uli, Izo ziyenera kuti ziwululidwe kwa iwe. Ndiye inu mukuwona Yemwe Yesu Khristu ali.

¹²⁴ Tsopano, apa, dongosolo lokonzedweratu liri pa mbalambanda. Mofanana ndi mbewu zina, Mawu a Mulungu ndi Mbewu ndipo nthaka iyenera kukonzedwa kaye. Ngati inu munafesa mbewu, kungoyiponya iyo pansu apo panthaka, izo sizikanachita ubwino uliwonse, mbalame zikanakhoza kuzitola izo. Mukayiponya iyo pakati pa nthula ndi minga, zidzayitsamwitsa iyo posakhalitsa. Fanizo la Yesu linanena zimenezo. Koteru nthaka iyenera kukonzedwa choyamba. Koteru, Mulungu, mu chisomo choyima pachokha, amakonzezeretsa mtima poyamba. Iye anakukonzekeretsani inu maziko a dziko lapansi asanakhale, kuti mumulandire Iye mu m’badwo uno. Iye anakudziwiranitu inu mwa kudziwiratu Kwake, ndipo anakudzodzani inu ku Moyo Wamuyaya. Iye anakudziwani inu, chotero Iye anakukonzekeretsani inu.

¹²⁵ Ndicho chifukwa chimene inu munadzandima kuchoka ku zinthu izi, ndi kudzandima kulowa mu zomwe muli nazo tsopano. Anali Mulungu akukutsogolerani inu ku malo kumene Iye anakuikirani inu kuti mukakhale. Iyo... kapena ngati—ngati—ngati nthaka iyi siinakonzedweretu, iyo siingathe kukula. Ndicho chifukwa chake, mbewu ya chikhulupiriro, pamene inu mukulalikira chikhulupiriro, kuwona kuzindikira za mmitima kwa Ambuye, ndi kuwona chimene chikuchitika, ndi mphatso zonse za Baibulo zikugwira ntchito. Anthu amadzikondoweza okha, “O, aleluya, ine ndikukhulupirira Izo,” ndipo nkubwerapo, ndipo amadzipeza okha okhumudwa. Mwawona, nthaka iyenera kukhazikitsidwiratu. Ndipo inu mukudziwa pamene Iyo ikhudza iyo.

¹²⁶ Monga mphungu yanga yaing’ono, usiku wathawu. Iye anadziwa pamene iye anamva kufuula kuja kwa mayi mphungu, “pali kusiyana kwakukulu pakati pa iko ndi kulira kwa nkukuku.” Mwawona, chifukwa iye anali mphungu kuchokera mu dzira. Osati... iye sanapangidwe mphungu pamene, iye nthawizonse anali mphungu. Ndipo Mkristu nthawizonse anali! Ndicho chifukwa chake, chilekano, pamene inu munasudzulana, chifukwa inu munakodwa mu izo, mwawona, mwa makolo anu oyamba, Adamu ndi Eva. Inu mumakhala wochimwa mwachibadwa. Inu simunafune kuti mukhale, koma tsopano inu munamva Uthenga, ndipo “chikhulupiriro chimadza pa kumva,” vumbulutso limadza pa kumva. Pali chinachake chaching’ono mkati mwa inu.

¹²⁷ Munthu wina atakhala pafupi ndi inu, kunena, “Ah, ine sindimakhulupirira zinthu zimenezo. Zamkutu! Ine sindimakhulupirira zimenezo. Palibe kanthu kwa izo!”

128 Monga iwo anachitira pa Tsiku la Pentekoste, iwo anaseka ndipo anati, “Anthu awa akhuta vinyo watopano.” Iwo ankadziwa kuti izo zinali. . . Chinali chinthu chachikulu kwa iwo omwe chinali kuwachitikira. Chifukwa chiyani? Anali Mulungu akudziwulula Yekha kwa aliyense payekha. Pamene ena ankaseka, awa anali akusangalala. Linali vumbulutso la munthu payekha, chimene chiri chikhulupiro; chikhulupiro chimene chawululidwa. Ngati icho sichinali chikhulupiro, ndiye iwo sakanakhalapo nkome. Icho chinali chikhulupiro.

129 Mbewu basi nthaka iyenera kukonzedwa poyamba. “Chotero, onse amene Iye anawadziwiratu, Iye anawaitana. Onse amene Iye anawaitana. . . Onse Iye anawadziwiratu, Iye anawakonzeratu.” Ngati inu mukufuna kuti muwerenge izo, Aroma 8:28-34, ndiponso Aefeso 1:1-5. Mwawona, onse amene Iye anawadziwiratu, Iye anawaitana. Onse amene Iye anawaitana, Iye anawalungamitsa. Ndipo onse amene Iye anawalungamitsa, Iye wawapatsa kale ulemerero. Palibe chomwe sichiri mu dongosolo. Ife timaganiza chilipo, koma tayang’anani mu Malemba. Izo zikungogunda ndendende momwe Mawu a Mulungu ananenera kuti izo zikanadzachitika. Ife tikuwona Uthenga ukukanidwa, lero. Kodi izo siziri basi zomwe Lemba linati iwo akanadzachita? Ndithudi, zinthu zonse izi ndi zoikidwiratu ndi Mulungu.

130 O, Izo ziyenera kukupangitsani inu kuyenda mosangalala. Ndilo vuto ndi ife lero, kusiyana kwakukulu ndi Akhristu akale. Pamene lenileni, vumbulutso loona la Yesu Khristu kukhala Emanuele linkakhala mmitima ya anthu amenewo, iwo anali anthu olimba. Koma lero ife tikusisitidwa ndi zipembezdo, ndi, “O, ine ndikukuuzani inu, iwo alibe Vumbulutso. Inu bwerani kuno.” Inu mukudalira pa vumbulutso *lawo*. Ngati vumbulutso lawo siliri molingana ndi Mawu a Mulungu, ndiye kuti ndi lolakwika; langa kapena la wina aliyense, ndi pamene chiwonetsero chimayambira. Mawu a Mulungu amatiuza chomwe chiri cholondola ndi cholakwika!

131 Mbewu iliyonse iyenera kukhala ndi nthaka yake, ndithudi. “Chotero, onse amene Iye anawadziwiratu. . .” Mwawona, Iye ankadziwa kale zomwe zinkati zidzachitike. Zindikirani, Yesu ananenanso, za Mbewu, “Zina zinagwera pa miyala, zina m’ malo osakanikirana.” Mwawona, pamene pali minga, nthula, ndi china chirichonse, Izo sizikanakhoza kumera. Ndipo zina pa nthaka yabwino, nthaka yabwino, dothi labwino, limene linali litakonzedwa kale, lokonzedwa kale.

132 Anthu onse kunjira kuno, iye ali ngati nkukhu, iye akuyang’ana motsatira, akuyesera kuti apeze. Iye amapita mu *ichi*, ndipo iye amapita mu *icho*, koma pakapita kanthawi pamabwera Mfuwu yadzidzidzi kuchokera Kumwamba. Iye amawuzindikira Iwo mwamsanga ndithu, “Ndiwo Mawu a Mulungu!” Mwawona, iye amawudziwa Iwo chifukwa pali

chinachake mu mtima mwake chimene chazidwa kwa iye, chowululidwa kwa iye za Iwo.

¹³³ Zindikirani, mneneri Yesaya anati, “Namwali adzaima.” Ndi mawu achilendo bwanji. Kodi mu—munthu wa malingaliro ake abwino anganene bwanji zimenezo? Sipanakhaleko konse namwali amene anaimako. “Namwali adzaima!” Tsopano, iye sanadandaule za kunena Izo, iye anangozinena Izo. Iye adzazichita bwanji izo? Chabwino, iyo si ntchito yake! Iye. . . Ndi kungonena zomwe Mulungu ananena kuti zichitika. Mulungu anamuwululira izo, anamuwonetsa iye masomphenya; anawulula izo, ndipo izo zinali zolondola.

¹³⁴ Mulungu yemweyo basi yemwe anandiuza ine kuti mwana wamng’ono uyo akanati adzabadwe ndi mwamuna ameneyo amene sakanatha kukhala ndi mwana, kapena kukhala ndi mtsikana. Monga enawo ndi zinthu, momwe izo zimamvekera zachilendo pamene adokotala amanena, “Izo sizingachitike!”

¹³⁵ Koma pamene Mulungu anena, “Izo zidzachitika,” izo zimatengera mtundu wa mawu omwe akugweramo. Kumbukirani, mneneri anayimirira pamene ndipo Mawu Ake anapita.

¹³⁶ Monga Mulungu, mu Genesis 1, Iye anati, “Pakhale kuwala. Pakhale *ichi*. Pakhale *icho*.” Analenga munthu mu chifanizo Chake Chomwe, chifanizo cha Mulungu Iye anawalenga iwo, mwamuna ndi mkazi, ndipo panalibe kanthu pa dziko lapansi apobe. Ndiye, ife tikupeza mu Genesis 2, apa, Iye anapanga munthu mu chifanizo Chake Chomwe. Panalibe munthu woti azilima nthaka, chitatha chilengedwe chonse. Chinali chiyani icho? Ndi Mawu Ake, Iye anali kuwayankhula Iwo. Ndipo pamene Iye anayankhula, Iye anati, “Pakhale kuwala.” Pakhoza kukhala kuti panali pasanakhalepo kuwala kwa zaka eyiti handiredi patsogolopo, pakhoza kukhala panalibe kuwala, koma Iye ananena Izo! Ndipo bola ngati Iye ananena Izo, “Pakhale mtengo wa kanjedza. Pakhale mtengo wa thundu. Pakhale *ichi*,” mbewu zimenezo zinali zikuwumbika pansu pa madzi amenewo. Uko nkulondola. Ndipo mu nyengo, mu nthawi, mu nyengo yake yomwe, iyo inabala! Izo sizingalephere; ndi Mawu a Mulungu. Izo sizingalephere basi. Izo zafotokozeredwa.

¹³⁷ Tsopano, tsiku lina, Mulungu anayankhula kwa munthu, maso ndi maso. Koma mu nthawi ya Mose, pamene moto unali kugwa, iwo anati, “Lolani Mulungu. . . Lolani Mose ayankhule; osati Mulungu, ife tikhoza kuwonongeka.”

¹³⁸ Kotero, Iye anati, “Ine sindidzayankhula kwa iwo motero kenanso. Ine ndidzawadzutsira iwo mneneri.” Umo ndi momwe dongosolo la Mulungu linaliri nthawizonse.

¹³⁹ Tsopano, apa pali mneneri ataima; tsopano, iye ali pansu pa kudzoza; iye sakuganizira za luntha lake, “Tsopano, dikirani miniti. Ngati ine ndikananena izo, chabwino, inu mukudziwa,

anthu angaganize kuti ndine wamisala.” Mwawona, limenero ndi luntha lake; pamenepo iye akumvetsera kwa Satana, monga momwe Eva anachitira.

¹⁴⁰ Ndipo bola ngati dokotala akunena kuti, “Inu simungakhale ndi moyo. Inu simungakhale bwino. Inu simungathe kuchita *izi* kapena *izo*.” Bola ngati inu mumvetsera kwa izo, Mbewu imeneyo sidzagwa konse mu nthaka ya mtundu umenewo ndi kuchita ubwino uliwonse. Izo sizingatheke. Koma pamene chinachake chikung’amba zonse za izo, ndipo Icho chikugwera mu nthaka yobzalidwayo, palibe kanthu kangakhoze kung’amba Izo.

¹⁴¹ Tsopano, ziribe kanthu izo zitenga nthawi yayitali bwanji, izo zidzachitika. Tsopano, Iye anati, “Namwali adzaima.” Kodi inu mumadziwa kuti zinali zaka eyiti handiredi izo zisanachitike? Mulungu anamudziwiratu mkazi, yemwe akanati adzakhale, lomwe dzina lake linali, kumene Mbewu imeneyo ikanati idzagweremo. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ndithudi, Iye anatero! Ndipo kuchokera mmimba yenyeni mukanadzatuluka chozizwitsa chachikulu ichi. Mulungu ankadziwa za izo, Iye anangoziwulula izo kwa mneneri Wake yemwe anali wokhulupirika ndipo anayankhula Mawu. Popanda ngakhale kuganiza za omwe Iwo anali, iye anangowanena Iwo. Iye sanayesere konse kuzilingalira Izo.

¹⁴² Ngati inu muyesa kulingalira...Bwanji ngati mwamuna uyu, mkazi uyu, kapena mwamuna uyu wakhala apa, kapena winawake ayesera kulingalira, “Tsopano, ine ndakhala wolumala zaka zonsezi. Dokotala akuti, ‘Palibe mwayi wothekera’”? Chabwino, mwina sungakhalepo molingana ndi momwe iye akudziwira, ndipo izo nzoona.

¹⁴³ Koma ngati chinachake chingang’ambe udzuwo, ngati Mulungu mwa chisomo Chake; osati mlaliki, osati wina aliyense. Koma Mulungu akhoza kuika mu mtima mwanu vumbulutso, kuti, “Ine ndikhala bwino,” palibe chimene chiti chidzakulepheretseni inu kukhala pamenepo. Palibe chomwe chingakugwireni inu pamenepo, inu mukhala bwino! Koma kufikira izo zitachitika, inu mukhala pomwepo pamene adotolo akuti inu mukhala; mpaka izo zitachitika. Izo zikuyenera kuwululidwa. Ndi chisomo cha Mulungu chimene chimawulula izo.

¹⁴⁴ Tsopano, zindikirani, Mulungu ankadziwa mkazi yemwe Izo zikanati zidzamufikire. Zindikirani Yesaya, panalibe funso. Yesaya sanati, “Dikirani miniti, Ambuye! Mundilole...Dikirani miniti yokha! Kodi Inu munati chiyani kwa ine, ‘Namwali adzakhala ndi pakati’? Chabwino, tsopano, tsopano dikirani, Atate, apo—apo—sipanakhalepo chinthu chotero monga icho chitachitika.”

145 Iye sanachedwechedwe, iye anangonena, “Namwali adzaima!” Kulondola.

146 Zindikirani Maria: “Tsopano, tsopano Ambuye, dikirani miniti. Inu mukudziwa, ine—ine sindinamudziwepo konse mwamuna. Izi sizingatheke! Palibe chonga ichi chinachitikapo! Ohhh, o, ayi, palibe chonga ichi chinachitikapo. Ine ndikhala bwanji ndi mwana ameneyu? Ine sindikudziwa mwamuna aliyense, kotero izo sizingachitike! Uh, Mngelo, inu mwangolakwitsa. Ine ndiri ndi zilubwelubwe. Inu mukudziwa, mpingo wanga umati, ‘Masiku ano anapita.’” Ayi! Izo sizikanagwera konse mmalo oterowo. Maria sanafunse konse.

147 Iye anati, “Zingatheke bwanji izo? Ine sindimudziwa mwamuna.”

148 Iye anati, “Mzimu Woyera udzakuphimba iwe. Umo ndi momwe zidzachitikire.”

149 Iye anati, “Tawonani, mdzakazi wa Ambuye!” Popanda funso!

150 Mwawona, Yesaya, pamene Mulungu anatulutsa Mawu mwa lingaliro (vumbulutso) kulowa mu mtima wa Yesaya, Iwo anagwera mu nthaka yoyenera, uyo anali mneneri. Mneneri ameneyo sanasamale nzeru za munthu aliyense. Iye sanasamale za luntha la munthu aliyense. Iye sanasamale za munthu wa aliyense. Iye anali mpita woperekedwa kwa Mulungu, ndipo Mulungu anayankhula ndipo iye anayankhula. Ndizo zonse. Kaya izo zinapweteka, kaya izo sizinatero; kaya izo zinkamveka ngati zopenga, kaya izo sizinamveke ngati zopenga; sizinapange kusiyana kulikonse kwa iye. Iye anali Mulungu, osati munthu.

151 Ndipo pamene Mawu amenewo anapita, tsopano Iwo amakhala Mbewu, Iyo imayenera kugwera penapake. Ngati Mulungu ananena Iwo, payenera kukhala chiberekero penapake kuti Iwo akagweremo. Monga momwe Iye ananenera, “Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira. Ngati iwe unena kwa phiri ili, ‘Suntha,’ ndipo nkusakaikira mu mtima mwako, iwe ukhoza kukhala ndi zimene iwe wazina.” Mwawona, pakuyenera kukhala penapake pamene pali polondola!

152 Zindikirani! Tsopano, ife tikupeza kuti Yesaya apa anayankhula Izo.

153 Namwali Mariya, mwamsanga pamene...Nthaka inali itasweka kale. Iye anali ali namwali. Iye anali “asanathamange mozungulira.” Nthaka inali itakonzedwa kale, kapena kuzonzedweratu mwa kudziwiratu kwa Mulungu.

154 Ngakhale anati, “Iye anali namwali.” Pomwepo Mulungu ankadziwa lomwe dzina lake likanadzakhala. Pakuti dzina lake linali pa Bukhu la Moyo Kumwamba.

155 Ndiye, Iwo anatsimikiziridwa. Munthu ndiye (kwa munthu) anawona kufotokozerwa kwa Izo mwa ntchito, pamene izo zinali zitachitidwa kale. Tsopano ife timayang’ana mmbuyo ndi kuti, “Ndithudi, Izo zinachitika,” chifukwa ife tikuwona ntchito zomwe zinachitidwa.

156 Ntchito za Nowa zinafotokozeredwa kwa munthu, chomwe chikhulupiriro chake chinali mu lonjezo la Mulungu. Tsopano, Mulungu anakumana ndi Nowa, ndipo Iye anati, “Nowa, mvula idzagwa. Ine ndidzawononga dziko lonse lapansi ndi madzi.” Tsopano, kunali kusanagweko mvula nkomwe, zimenezo zinali zosatheka. Chabwino, tsopano, Nowa anatenga. . . Anati, “Konza chombo cha miyezo yomwe Ine ndidzakuuza iwe.” Ndipo iye pokhala kalipentala, ndipo iye anapita kuti akagwire ntchito ndi kuyamba kutenga sopho yake, ndi chirichonse kuti azidula matabwa, ndi kuzikonza izo pamwamba apo ndi matabwa a njale, ndi kuika phula mmenemo monga momwe Iye ananenera. Ndipo kodi inu mukuganiza kuti anthu ankaganiza chiyani za munthu ameneyo?

157 Iwo anati, “Munthu ameneyo ndi wopenga kwenikweni, chifukwa iye akuti, ‘Idzatulutsa madzi kuchokera kumwamba,’ ndipo mulibe madzi mmwamba mmenemo.” Koma, inu mukuwona, Nowa sanaganize za zimenezo. Ntchito zake zinali kufotokoza kwa anthu chomwe chikhulupiriro chake chinali ndi zomwe Mulungu ananena kuti zikanadzachitika.

158 Ndicho chifukwa chimene Mkristu weniweni amadzapatula yekha ku chirichonse kupatula Mawu a Mulungu, ziribe kanthu zomwe anthu akuganiza, chimene wina aliyense akunena. Iye anzilekanitsa chifukwa. . . Iye sakungonena zimenezo; ngati iye akutero, sipatenga nthawi mpaka ntchito zake zidzadziwika. Iye adzagwera mmbuyo ndi kutsetserereka mbali *iyi*, ndi kujowina *izi* ndi *izi*. Ndi kuyamba. . . Iye adza—iye adzawonetsera chomwe iye ali. Koma ngati iye ali weniweni, ngati Mawu a Mulungu adzalidwa mwa iye, ndiye Iwo adzabala za mtundu Wake, inu mudzamuwona munthu ameneyo akukonzekera ora lalikulu limenero. Mwawona, umo ndi momwe Nowa anachitira.

159 Mose, ndi ndodo m’dzanja lake, anabwera kudzatenga anthu kuchokera kwa Farao. Tsopano, kodi inu mungalingalire. . . Mose, Baibulo linanena kuti iye anaphunzitsidwa mu nzeru zonse za Aigupto. Iye anali wanzeru, iye amakhoza kuphunzitsa zinthu zawo zaluntha. Iye anaphunzitsidwa mu nzeru zawo zonse. Iye sankasowekera kuti akambirane pa maphunziro ake. Tsopano, inu tangoganizani za mwamuna kunja uko mchipululu, ndi maphunziro onse amenewo, ndipo kenako Mulungu akuwonekera kwa iye ndipo anati, “Mose, tenga ndodo iyi mdzanja lako, nutsikire kumeneko ku Aigupto, ndipo ukatulutse ana Anga ndi ndodo iyi yomwe uli nayo mdzanja lako. Ukangowumbudza chinthu chonsecho ndi ndodo iyi.”

160 Tsopano, bwanji ngati Mose akanati, “Bwana, mphindi yokha, ine ndimaganiza kuti ine ndikuyankhula kwa Munthu wanzeru, ‘INE NDINE wamkulu uyu amene Inu mukuti Inu muli. Tsopano, ine mu dziko ndingatenge bwanji ndodo yaying’ono, yakale, yokhota iyi yomwe ine ndiri nayo apa mu dzanja langa, ndi kukagonjetsa gulu lankhondo la mamiliyoni a anthu, lokhala ndi mikondo, ankhondo? Ndipo ine sindine wankhondo, ndine m’busa. Ine ndingachite bwanji zimenezo?”

161 Panalibe funso! Chifukwa chiyani? Chifukwa chiyani? Nthaka mu mtima mwake! Iye anali munthu wokonzedweratu. “Mphatso ndi maitanidwe ziribe kulapa.” Mulungu anali atamuza Abrahamu kuti Iye akanadzachita zimenezo, ndipo apo panali nthaka yokonzedwa.

162 Ndipo Mose anatenga ndodo iyi ndipo anapita kumusi uko ndipo analitenga fuko limenero kuchokera mu fuko. Pamene iye anabwera ndi ndodo mu dzanja lake, ndipo anamuza Farao, “Alole iwo azipita!” Farao anawona mwa Mose ntchito, kuti iye anali nacho chikhulupiriro mu chimene iye ankati achite, kapena kuyesera kuchita. Iye anali ndi chikhulupiriro mu lonjezo la Mulungu yemwe anali atapanga lonjezo, iye anapita kumusi kuti akalitenge ilo. Panalibe munthu wina akanachita izo, ndipo panalibe munthu wina akanachita izo, iye anadzozedwa kuti achite izo. Mulungu, kale, anali atamuza Abrahamu kuti ndi zomwe zikanadzachitika. Ndipo pamene nthawi ya lonjezo inayandikira, apo panali mnyamata wamng’ono atabadwa, mwana wokongola. Ndipo makolo ake, Amramu ndi Yokebedi, sanawope malamulo a mfumu. Mwawona, panali chinachake, nthaka inali itakonzedwa kale.

163 O Mulungu, ine ndikuyembekeza ndikuyankhula kwa nthaka yokonzedwa, usikuuno! Ngati Mbewu ingakhoze kugwera pa malo oyenera, ndipo izo zikhala zina-... Ngati sichoncho, izo sizichitika.

164 Ndicho chinthu chomwecho. “Bwanji,” inu mukuti, “M’bale Branham, zimenezo zimachita ngati zimazichotsa izo kwa ife.” Ngati izo zimatero, izo zimachotsa izo ku Chikristu, nazonso. Mwawona, inu mukhoza kutsanzira chirichonse. Koma ngati... Ngati Iwo agweramo kwenikweni, Mawu a Mulungu agwera mu nthaka yoyenera, Iwo adzabala za mtundu Wake. Izo zikuyenera kutero, chifukwa Iyo ndi Mbewu.

165 Nowa... Mose, ntchito zake zinkasonyeza chikhulupiriro mu lonjezo la Mulungu amene iye anamukhulupirira. Farao, munthu, amakhoza kuwona chimene chinali... ayi... iye sankakhoza kuwona momwe Mose akanachitira izo, koma iye ankadziwa kuti Mose ankakhulupirira zimene iye ankazinena kapena iye sakanaima mnyumba ya mfumu ali ndi ndodo mu dzanja lake. Anati, “Ndi ndodo iyi, ine ndiwatulutsa iwo kuchoka kwa inu.” Munthu wokalamba, zaka eyite, osati

wothamanga; munthu wokalamba, wamapewa-akugwa, ndi ndevu zikulendewera pansu kwa iye, mwinamwake, mchiuno mwake; tsitsi laimvi, ngati iye anali nalo. Ndipo pamenepo ali ndi ndodo imeneyo mdzanja lake, akuti, “Ine ndiwatulutsa iwo, muwalole anthuwa azipita,’ PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndipo ngati inu simuchita izo, Mulungu akuweruzani inu.” Ameni! Chifukwa chiyani? Ndiko, mwawona, iye, kodi iye ankachita mantha? Bwanji, mpaliro umodzi wokha, mkondo umodzi, china chirichonse chikanathetsa izo. Iye anali wopanda mantha! Iye ankadziwa ndendende pamene iye anali kuyima; anati, “Mulungu akukantha iwe Farao.” Inde, bwana.

¹⁶⁶ Pakuti Mulungu anamuza iye kuti, “Udzabweranso kuphiri ili,” ndipo iye ankadziwa kuti iye anali kupita kumeneko.

¹⁶⁷ Aleluya! Ife tikudziwanso komwe ife tikupita nafenso, kumapeto kwa ulendo uno. Mulungu walonjeza! Pali Dziko kutsidya la mtsinjewo. Khalani opanda mantha mu umboni wanu. Ameni. Ngati zawululidwa kwa inu, inu mumakhala opanda mantha. Inu simusamala ngati dziko lonse lapansi... zimene iwo amanena; ndinu wopanda mantha. Pamene zawululidwa kwa inu, kuti, “Ichi ndi Choonadi chochokera kwa Mulungu,” ndiye inu mudzakhala wopanda mantha. Ngati sichoncho, inu simungakhale.

¹⁶⁸ Davide, ndi legeni ya m’busa, anafotokozera kwa gulu lonse lankhondo la Israyeli, chikhulupiriro chimene anali nacho mwa Mulungu wawo. Tsopano, apo panali Goliati ku mbali inayo, ndipo iye anayima kunja uko ndipo anapanga kudzitukumula kwake. Wamkulu kwambiri zedi kuposa Davide, iye anali ndi zala mainchesi fortini kutalika. Ndipo iye anali wokulupala, munthu wamkulu, chimphona cha Afilisti. Ndipo apa panali Davide, wamng’ono kwambiri, iye anali ngakhale wamng’ono kwambiri kuti akhale mu gulu la ankhondo; anali wamng’ono kwambiri, iwo sakanatha kumugwiritsa ntchito iye. Koteri, abale ake anali kunja uko mu gulu la ankhondo. Ndipo, ndiye, Goliati anali kupanga kudzitukumula kwake.

¹⁶⁹ Koma Davide, tsopano kumbukirani, izo zinawululidwa kwa Davide. Iye anaganiza, “Pano pali magulu ankhondo a Mulungu wamoyo, akuima mu dziko lawo lomwe, ndipo apo pali Mfilisti wosadulidwa wodzitukumula kunja uko.” Ife timutcha iye “khansa” usikuuno, ife timutcha iye “kupuwala.”

¹⁷⁰ Bwanji, Davide sanali ngati wofanana naye iye, wosakhala ndi mtundu uliwonse wa chida; iye sanali wofanana naye. Mapewa a munthu ameneyo mwina anali teni, mapazi thwelofu kupingasa; iye mwinamwake anali ataima mapazi fortini, mapazi fiftini kutalika. Mkondo wonga singano ya woluka, mwinamwake utali wa mapazi twente, mpeni wake ukhoza kukhala mapazi foro kupingasa.

¹⁷¹ Ndipo Davide wamng'ono atayima pamenepo ali ndi kachidutswa kakang'ono ka chikopa, chikopa cha mbuzi kapena chikopa cha nkhosa, ndi zingwe ziwiri zomangiridwa ku iko. Koma izo *zinawululidwa* kwa iye! Vumbulutso linamukantha iye! Ameni! Iye anati, “Mulungu amene ananditulutsa ine mmapazi a chimbalangondo, amene ananditulutsa ine mmapazi a mkango, ndi mochuluka bwanji momwe Iye adzapereke Mfilisti wosadulidwa ameneyo mdzanja langa!”

¹⁷² Abale ake, okhoza mochuluka kuchita izo. Sauli, mutu ndi mapewa pamwamba pa gulu la ankhondo ake. Koma, inu mukuwona, izo sizinawululidwe kwa iwo. Ameni. Ndi izo apo: iwo ankakhulupirira kuti izo zikanatheka, iwo ankakhulupirira kuti Mulungu akanakhoza kuchita izo, koma izo sizinawululidwe kwa iwo; koma izo zinawululidwa kwa Davide. Tsopano, apo pali kusiyana, apo pomwe. Ngati izo mwamtheradi zawululidwa kwa inu kuti Mulungu akuchizani inu, inu—inu muzipeza izo. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] Inu muzipeza. . .Ine sindikusamala chomwe chiri cholakwika ndi inu, momwe mwai uliri, izo chikhoza kukhala moyipitsitsa kuposa Davide ndi Goliati. Koma ngati izo zawululidwa kwa inu!

¹⁷³ Ndipo zindikirani, pamene izo ziwululidwa, Davide anakhala wopanda mantha. Iye anati, “Lero ndidula mutu wako!” Ameni. Ameneyo ndi Mulungu wathu. Mwa chisomo, mu nthawi yovuta imeneyo pamene zisankho zinkayenera kupangidwa, Mulungu yemweyo amene anapereka chisomo mu tsiku limenero, ndipo anagwetsera mbewu ya chikhulupiriro imeneyo mwa mnyamata wamng'ono wowoneka ngati kanjipiti, pokhala mu mtima mwake; Mulungu yemweyo, mu mphindi yovuta iyi, akhoza yumuchotsa mkazi uja kuchoka pa chikuku; mwamuna *uyu*; mkazi *uyu* apa; mwana; a . . .? . . . Njere yaing'ono iyo ya chikhulupiriro yawululidwa kwa inu, ndiye ine sindikusamala izo zitenga nthawi yayitali bwanji.

¹⁷⁴ Tsopano zindikirani chimphona, mbali inayo, sichinakhulupirire izo; ngakhalenso khansa. Iye anaseka, iye anati, “Kodi ndine galu? Inu mukutumiza mwana ameneyo kuti adzamenyane nane?” Anati, “Ine ndidzakunyamula iwe pa nsonga ya mkondo wanga, ndi kulola mbalame zidye mnofu wako.” Bwanji, iye anali nazo zonse. . .zonse, zonse kumbali yake.

¹⁷⁵ Koma, inu mukuwona, izo sizinamugwedeze Davide nkomwe. Chifukwa chiyani? Izo zinawululidwa kwa iye. Iye anali ndi chikhulupiriro mu zimene iye anali kuchita. Iye anadziwa kuti iye adzachita izo. Ndipo iye anachita izo, ndi chifukwa chakuti izo zinawululidwa kwa iye ndipo iye ankadziwa pamene iye ankayima.

¹⁷⁶ Ndipo ngati Mulungu akanangoyankhula zimenezo, pansi

mu mtima mwanu usikuuno, nati “Inu simudzagona pa bedi limenero. Inu simukhala mu mpando umenewo. Inu mukhala bwino,” apo sipakanakhala chirichonse chingasithe malingaliro anu mu izo.

177 Koma mpaka izo zitachitika, mlaliki aliyense mu dziko akhoza kupemphera, . . . Ine sindikuti izo sizingakuthandizeni inu; izo zingatero, izo zingakulimbikitseni inu. Koma mpaka chikhulupiriro chimenecho. . . Mwawona, mphamvu yochiritsa ili mwa inu. Iyo simachokera kwa mlaliki. Iyo imabwera kwa inu mwa vumbulutso, mwa chikhulupiriro. “Si mphamvu, si nkondo, koma mwa Mzimu Wanga,” atero Ambuye. “Mzimu Wanga, mwa chisomo, umawulula izi kwa inu.” Ndipo palibe chomwe chingazichotse izo. Mwa chikhulupiriro, vumbulutso! Kenako, Davide kuti atsimikizire ntchito zake, . . .

178 Tsopano, ena a iwo anati, “Ine ndikudziwa ndiwe wamwano.” Mchimwene wake anati, “Iwe wabwera kuno kudzawona nkondo. Tsopano, iwe ubwerere kumene nkhosa zimenezo zinali.”

179 Iye anati, “Ndiloleni ine ndiyankhule kwa Sauli, mkulu wankhondo.” Inu mukuwona?

180 Ndipo Sauli anati, “Tsopano, mwana, ine ndikuyamikira kulimba mtima kwako, koma, iwe ukuwona, sindiwe kanthu koma wachichepere. Ndipo iye ndi wankhondo kuyambira ubwana wake, iwe sungafanane ndi iye.”

181 Iye anati, “Ine ndinali kuweta nkhosa za atate wanga, . . .” Iye amakhoza kuzikhazikitsa izo pa chinachake! Ameni. O m’bale! Ndipo Mulungu amene anapulumutsa moyo wanu, kodi Iye sangakhoze kuchiza thupi lanu? Ziri chimodzimodzi basi, kuwulula kwa inu, Iye ndi Mchiritsi wanu monga Iye anali Mpulumutsi wanu. Mukuwona? Koma izo ziyenera kuwululidwa poyamba, ndiko kusiyana kwake. Iye anali ndi chinachake choti akhazikitsepo chikhulupiriro chake.

182 Anati, “Tsopano, izi sizinachitikepo kale.”

183 Koma anati, “Mulungu yemweyo amene anandipulumutsa ine kuchokera ku mapazi a mkango, andilanditsa ine kwa Mfilisti wosadulidwa ameneyo.”

“Iwe ukudziwa bwanji, Davide?”

“Ine ndikukhulupirira izo.”

“Chifukwa chiyani?”

“Izo zawululidwa kwa ine.” Ndipo iye anati. . .

184 Iye ankadziwa zomwe iye ankazinena. Chifukwa pamene chimphonacho chinati, “Ine ndikudyetsa iwe kwa mbalame”; iye anati “Ine ndikudula mutu wako.” Apo pali kusiyana, mwawona. Ndipo iye anachita izo!

¹⁸⁵ Samsoni, anagwidwa tsiku limodzi (mosayembekezera) mu chipululu, ndipo apa panadza Afilisti chikwi pa iye. Ndipo iye anayang'ana pansi, ndipo apo ndi pamene bulu anaferapo, ndipo iye anatola fupa lakale, chibwano, chowuma momwe icho chikanakhoza kukhalira, ndipo anapita kuwatsatira Afilisti aja, kuwamenya iwo pa mutu ndi fupa la chibwano chakale chowuma cha bulu chimenechi, ndipo monga momwe ine ndikudziwira, panalibe ngakhale dzino lomwe linagwa kuchokera pa icho. Ndipo zipewa za Afilisti izo mwina zinali zokhuthala inchi (chifukwa iwo ankamenyana wina ndi mzake ndi zibonga zankhondo mmasiku amenewo), kuti munthu asawamenye iwo pamutu. Koma iye anatenga fupa la chibwano cha bulu chija ndipo akanantha Afilisti sauzande, ndipo fupa la chibwano silinathyoke. Iye ankangopitirira kuwamenya iwo, monga *choncho*, pamene iwo ankabwera. Kotero, ena onsewo ananyamuka kupita ku mathanthwe, mwawona, iwo ankachoka kwa iye. Chifukwa chiyani? Iye anakhulupirira izo! Nthawi zina... Ndithudi.

¹⁸⁶ Ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu chinachake tsopano. Gwirani ntchito pa kugunda uko, ka mpata kameneko ka mphindi, monga Yoswa anachitira, monga Mariya Magadala, onse awo. Nthawi yomweyo pamene chinachake chawululidwa kwa inu, chigwireni icho. Gwiritsitsani ku icho, ka mpata kameneko ka mphindi.

¹⁸⁷ Inde, izo zinawululidwa kwa iye. Iye anapita kukakumana ndi masauzande awa, Afilisti. Tsopano inu mukuganiza chiyani pamene Afilistiwo anati, "Tsopano, yang'anani, akubwera apo, ka nthumbidwa kakang'ono kameneko; pafupifupi mapazi anayi ndi theka basi kutalika, kuyamba ndi kuyamba; ali ndi njombi seveni zazing'ono zikulendewera kumbuyo kwake, monga mwana wa amayi wachikazi, mwawona; akubwera kumeneko ndi fupa la chibwano cha bulu. Ndipo tayang'anani pa ife, ndife gulu lalikulu lankhondo bwanji! Kodi zimenezo sizopusa?" Koma kodi iye anali kuchita chiyani? Iye anali kufotokozera kwa Afilistiwo chimene chinali chitawululidwa kwa iye ndi Mulungu. Iye anagwira fupa la chibwano ndipo ananyamuka, chifukwa ndicho chimene Iye anachiyika mu dzanja lake; Iye anaika icho mu dzanja lake, ndicho chimene iye ankakhulupirira: iye akanakhoza kuchita izo! Ndipo pochita zimenezo, iye anali kufotokozera kwa Afilistiwo chimene Mulungu anaika mu mtima mwake kuti achite.

¹⁸⁸ Yohane M'batizi anafotokozera chikhulupiriro chake mwa ntchito zake, ndi pamene iye ananena "Apo pakuyima Mmodzi pakati panu tsopano." Tangoganizani za izo. Yohane Woyera, ine ndiri nalo Lemba, Yohane Woyera 1:26, mwawona. Iye anati...

¹⁸⁹ Iwo anati, "Iwe ukuti, 'Mesiya akubwera'? Bwanji," iye anati, "munthu, chavuta ndi chiyani ndi iwe? Ife takhala tikumufunafuna Iye kwa zaka foro sauzande."

190 Iye anati, “Iye wayima pakati panu pomwe pano.” Aleluya! Koteru Iye ali usikuuno! U-nhu.

191 Iye anafotokozeru chikhulupiriro chake mwa vumbulutso lake, chifukwa izo zinawululidwa kwa iye kuti . . . iye ankadziwa kuti iye akanati adzamubatize Mesiya. Iye anali munthu, usinkhu wa zaka sarte. Iye ankadziwa kuti Iye ankayenera kukhala kumeneko kwina kwake; iye anali asanadziwe konse yemwe Iye anali, ndipo apo Iye anali atayima pakati pawo pomwe. Iye anati, “Apo pali Mmodzi waima pakati panu tsopano, Yemwe inu simukumudziwa, ndipo ine sindine yoyenera kumasula zingwe za nsapato Zake, koma Iye adzakubatzani inu ndi Mzimu Woyera. Ndipo Iye ali pakati panu tsopano.” Iye anafotokozeru izo, chikhulupiriro chake, chifukwa iye ankadziwa, mu tsiku lake, iye anali woti adzawone ndi kumubatiza Mesiya wa Mulungu. Koteru, inu mukuwona, anthu ankakhoza kuwona kafotokozedwe kake pa iye, mu njira yomwe iye ankalalikirira ndi momwe iye ankachitira, ankafotokozeru kuti iye anali ndi vumbulutso loona lochokera kwa Mulungu.

192 Tsopano, kuti atsimikizire kuti izo zinali zoonu, akuyenda kutuluka mu gululo pakubwera Mesiya; mnyamata wamba chabe akuyenda kudutsa kumeneko, atavala monga munthu wina. Yohane anati, “Tawonani, apo pali Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo la dziko lapansi.”

193 “Kodi iwe wamudziwa bwanji Iye?”

194 Iye anati, “Iye amene ananenu kwa ine m’chipululu, ‘Pa Iye amene iwe udzawona Mzimu ukutsika, ndiye Mmodziyo amene adzabatize ndi Mzimu Woyera.’”

195 Mwawona, iye ankamudziwa Iye chifukwa pamayenera kukhala chizindikiro cha nthawi imeneyo. (Kodi mukuzigwira Izo?) Yohane anadziwa basi pafupifupi oralo, chifukwa iye anali mneneri. Izo zinawululidwa kwa iye, kuti iye ankadziwa kuti zikanadzakhala pafupifupi nthawi imeneyo, iye akanadzawona chizindikiro. Ndipo pamene iye anawona chizindikiro chimenecho, iye anati, “Iye wayima pakati panu.” Iye ankadziwa kuti Iwo unali pamenepo.

196 O, ine ndikuwona chizindikiro kuti nthawi yotsiriza yafika. Ine ndikuwona zinthu zomwe zalonjezedwa, za Uthenga wa nthawi yotsiriza uwu, zikufika pochitika (kufutukuka) chimodzimidzi basi monga Lemba linanenera. Ndipo ine ndikudziwa kuti nthawi yayandikira! Ine ndikunenu zimenezo popanda chikaiko. Ine ndikukhulupirira izo ziri pafupi kumene, pakuti ine ndikuwona zizindikiro zimene Iye anati zikanati zidzachitike isanafike nthawi imeneyo. Izo zakonzeka kuti zichitike *tsopano*.

197 Yohane anafotokozeru chikhulupiriro chake pa zimene Mulungu anamuwululira iye. Koteru, ntchito ndi umboni wa

chikhulupiriro. Pamene iwo akuwonani inu mukuchita ngati mwachiritsidwa, ndiye iwo adzadziwa kuti inu muli nacho chikhulupiriro kuti inu mwachiritsidwa.

¹⁹⁸ Kodi umboni umati chiyani? Kunena izi: “Ine ndiri nawo tsopano, chifukwa ine ndalandira lonjezo la Mulungu. Iwo tsopano akugwira ntchito mwa ine. Ine ndikukonzekera kuti iwo achitike.” U-nhu. Mwawona, ndicho chomwe umboni wanu- . . . ntchito zanu zimagwira. Chabwino, ndithudi!

¹⁹⁹ Kuno, nthawi ina kalelo, pafupi ndi ulendo wanga wotsiriza wa ku Africa; Ine ndinali kumeneko chilimwe ichi, koma ulendo wapambuyo pake. Panali mwana wamng’ono yemwe anali ndi mapazi obulungira, ndi phazi limodzi. . . mwendo waufupi kuposa unzakewo. Iye anali asanavaleko nsapato mmoyo wake. O, iye anali wopunduka moyipa kwambiri. Ndipo ine ndinamupempherera mwanayo usiku umenewo, iwo anali atayang’ana ndipo anawona zinthu izo zikuchitidwa, iwo anamupempherera mwanayo. Ndipo mmawa wotsatira ine ndinapita uko, ndinayenda pafupi ndi sitolo yogulitsa nsapato. Ndipo ine ndinalowa mmenemo, ndipo apo panali bamboyo akumugulira mwanayo nsapato kuti azivala. Iye anakhulupirira izo! U-nhu.

²⁰⁰ Monga bambo uyu cha kuno, yemwe ankakhulupirira kuti Mulungu akanamupatsa iye mwanayo. Ndithudi, iye ankakhulupirira kuti izo zikanadzachitika, anapanga kukonzekera izo. “Ine ndikukonzekera.” Ngakhale palibe zotsatira zakuthupi zomwe zinawonedwa pano, koma zimenezo sizinapange kusiyana nkome. Iye anakhulupirira izo, monga Abrahamu, “anatcha chirichonse chotsutsana ngati kuti sichinali chomwecho.” Pamenepo!

²⁰¹ Chifukwa chake, ngati aluntha anu akuuzani inu. . . O, apa pali choluma tsopano. Ngati aluntha anu akuuzani inu kuti “Tchi ndi Choonadi, Mulungu ndi Mchiritsi wa matenda,” malingaliro anu akhoza kuchitira umboni kuti “Chimenecho ndi Choonadi,” koma ngati mulibe pobzalapo mu mtima mwanu (chikhulupiriro, kuti chigweremo) kuti chifotokozere izo, izo sizichitika.

Osati kwambiri. . . ziribe kanthu kuchuluka kwa momwe munthu wakunja uyu angakhoze kulingalira izo ndi Malemba, ndi kunena, “ndi zolondola,” izo sizimapangabe izo kukhala zolondola.

²⁰² Ndi angati amatenga matepi? Kodi inu munaupeza ulaliki wanga, osati kale kwambiri, *Iwo Odzozedwawo A Tsiku Lotsiriza?* Kodi inu munazikhulupirira zimenezo? Mwawona, iyo inati, “Padzakhala otsutsakhristu. Otsutsakhristu akanati anyenge osankhidwa omwe, ngati nkotheke.” Sangathe izo, kuti. . . Koma sangathe, chifukwa ndi zosatheka; iwo ndi osankhidwa. Mukuwona? Chabwino.

²⁰³ Koma Iye anati, “Odzodzedwawo.” Mwawona, *Khristu* amatanthauza “wodzodzedwa,” koma awa anali otsutsa. Iwo anali odzodzedwa, koma otsutsa, otsutsana ndi *Khristu* mu chiphunzitso chawo. Tsopano, iwo akanakhoza kuchita chirichonse chimene ena onsewo akanachita.

²⁰⁴ Tsopano, kumbukirani, inu muli mu mkombero wa atatu, koma ndinu munthu mmodzi. Monga Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, mkombero wa atatu, koma Munthu mmodzi. Zikhumbo zitatu za Mulungu yemweyo: utate (maudindo atatu, monga), utate, umwana, ndi Mzimu Woyera. Ndipo inu ndinu: thupi, mzimu, ndi solo.

²⁰⁵ Tsopano, thupi lakunja liri ndi zolowera zisanu kwa ilo, kuti likhudze kwanu kwapadziko lapansi: kuwona, kulawa, kukhudza, kununkhiza, ndi kumva. Wamkati, umene uli mzimu, iwo uli ndi zokhudzira zisanu: chikumbumtima, ndi chikondi, ndi zina zotero. Koma mkati mwa izo, solo, ili ndi chinthu chimodzi. Ndiko komwe *inu* mumakhala.

²⁰⁶ Mzimu ukhoza kubwera kuno ndi kukudzodzani inu kuti muchite zinthu zinazake, ndipo inu nkuzichita izo, koma izo sizikutanthauza kuti inu mwapulumsidwa. Taganizani za izo. Kayafa analosera. Yudas anatulutsa ziwanda. Mwawona, Mzimu unamudzodza iye. Mvula iyi imagwera pa olungama ndi osalungama, namsongole akhoza kumasangalala pamodzi ndi tirigu. Koma ndicho chimene chiri pa chiyambi. Pamene ndi pamene inu mungakhoze...aluntha akhoza kuvomereza izo, kunena, “O, ndithudi, izo zikuoneka zabwino. Ine ndikukhulupirira zimenezo.” Izo sizimachitabe izo. Ayi, bwana. Ndipo mzimu ukhoza kuchitira umboni za izo, ndipo komabe siziri chomwecho. Chifukwa ngati solo imeneyo sinabwere kuchokera kwa Mulungu, iyo ikhoza kupanga zotsanzira zonse kunja kuno, koma izo sizingakhoze kukhala zenizeni. Inu mukhoza kuyerekeza machiritso, inu mukhoza kuchita ngati inu muli nacho. Inu mukhoza kuchita ngati mwachilandira icho. Akhristu akhoza kuchita ngati ndi Akhristu, ndi kumachita ndi kukhala abwino kwambiri pa izo, koma izo sizikutanthauza kuti iwo ndi opulumutsidwa. Ndiko kulondola ndendende, mwawona. Mzimu ukhoza kukhala pamene, weniweni, Mzimu weniweni. Mzimu Woyera ukhoza kukudzodzani inu, izo apobe sizikutanthauza kuti ndinu opulumutsidwa. Ndi solo yamkati iyo yomwe simafa, iyo ili nawo Moyo Wamuyaya. Iwo nthawizonse unali Moyo Wamuyaya. Mukuwona? Iyo imachokera kwa Mulungu, iyo imapita kwa Mulungu, ndi solo.

²⁰⁷ Tsopano, zindikirani izo, izo ziyenera kukhala. Faivi, c-h-i-k-h-u-l-u-p-i-r-i-o, kunja; mzimu, Y-e-s-u; mkati, i-n-u. Mukuwona? Umo ndi momwe kuyima pano, kuyang’ana pa inu, ine sindimadziwa mmodzi wa inu. Mzimu ukhoza kundidzodza ine, komabe ine sindikudziwa aliyense wa inu. Koma pamene wamkati mwa wamkati atulukirapo, ameneyo ndi Mulungu.

208 Ndi pamene wakunjayo angakhoze kulingalira. Inu mumutenge munthu, ndikuti, “Chabwino, inu mukudziwa, ine—ine ndikudziwa sindikuyenera kuti ndizichita chigololo. Koma, inu mukudziwa, ndiye mzimu umandiuza ine kuti ndisamachite chigololo. Koma, inu mukuwona, mmusi mmenemo mukadali chinthu chimenecho mmenemo.” Mwawona, izo zimakhala ngati zikulamulira mozungulira, ndipo kulibwino kuziyang’ana izo.

209 Koma pamene izo zilondoleredwa kuchokera mkati, izo zimaponyera zina zonsezo pamodzi. Chimenecho ndicho chikwangwani. Ndiyo nsanja yolamulira, wamkati mwa wamkati. Solo imalamulira mzimu, mzimu umalamulira thupi.

210 Koteru kuwalitsa kwakunja sikumapanga kusiyana kulikonse. Anthu achipembedzo amenewo kumbuyo uko, amene Paulo anawatcha “makoma owalitsidwa,” ndi zina zotero, iwo anali, akunja, basi njira iliyonse ya wo—wokhulupirira, ndipo iwo anali nawo mauneneri pakati pawo, ndi china chirichonse koma *mkati mwa wamkati* (“solo imene siimakhulupirira”).

211 Ndicho chifukwa chimene ine ndimati anthu akhoza kudumphama mmwamba ndi pansu, ndi kuyankhula mmalirime, anthu akhoza kufuula, kuika manja pa odwala, ndi kuchiritsa odwala ndi zina zotero, mwa chikhulupiriro; zinthu zazikulu zonse izi uko mwa Mzimu, nkukhala otayikabe. Iwo odzodzedwawo.

212 Zindikirani, Yesu anati, “Kungokhulupirira, pakuti zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira.” Chikhulupiriro ndi ntchito ndi mwamuna ndi mkazi, zimagwirira ntchito limodzi. Mwamuna amagwira ntchito ndi mkazi, mkazi ndi mwamuna; iwo amazindikira wina ndi mzake.

213 Monga mwamuna akunena kuti iye ndi “wokwatira” komabe iye osamatha kutulutsa ndi kuwonetsera kuti iye ali ndi mkazi, inu mumakayikira zonena zake. Um-hum. Mwamuna anati, “Ndine wokwatira.”

“Mkazi wako ali kuti?”

“O, o, ine—ine sindikudziwa za *izo*.” Mwawona? Mwawona? Chikhala ngati chinthu chovuta kwa ine kuti ndimukhulupirire iye.

Ine ndikuti, “Mkazi wako ali kuti?”

“Chabwino, ine sindikudziwa.” Ine—ine sindizikhulupirira izo.

214 Koteru, inu mukuwona, ngati inu muli ndi zomwe inu mukunena kuti inu muli nazo, “Ine ndiri ndi chikhulupiriro,” inu mudiwonetsa bwanji ine kuti muli nacho chikhulupiriro? Ndi ntchito zanu. Mwawona?

“Ndine wokwatira.”

“Ine ndidziwa bwanji kuti ndinu wokwatira?”

“Uyu ndiye mkazi wanga.” Mwawona? Ndi zimenezotu.

“Ndine wokwatiwa, uyu ndiye mwamuna wanga.”

“Ndachiritsidwa.”

“Iwe ukudziwa bwanji?”

²¹⁵ “Ntchito zanga zimasonyeza chikhulupiriro changa.” Mukuwona? Mukuwona? Tsopano, chimene—chimene inu mukuchikamba: chikhulupiriro chanu ndi chimene Mulungu amawona mwa inu, ntchito zanu ndi zimene anthu ena amawona mwa inu.

²¹⁶ Ndiko kusiyana pakati pa Yakobo ndi Paulo apa, akufotokoza za Abrahamu. Iwo sankatsutsana nkomwe wina ndi mzake, iwo anali onse ofanana; okwatirana.

²¹⁷ Chimodzimodzinsu chikhulupiriro chimene sichibala ntchito, aliyense ali ndi ufulu wokayikira umboni wanu. Tsopano, kodi inu mukuzimva izo? ife tisanayambe mzere wa pemphero. Ngati chikhulupiriro chanu sichibala ntchito ndi icho, inu simungakhoze kumupangitsa aliyense kukhulupirira kuti inu mwachiritsidwa. Nenani, “Chabwino, ine sindikudziwa.” Mukuwona? “Bwanji, eya, ndithudi, ine ndiri nacho chikhulupiriro chonse mu dziko lapansi.” Inu mulibe. Chifukwa, ngati inu muli, muli nacho chikhulupiriro, ndiye ntchito zimakwatiwa ndi chikhulupiriro. Izo ndi mwamuna ndi mkazi, wina—winayo amamuzindikiritsa winayo.

²¹⁸ Tiyeni tiganizire za Abrahamu kwa maminiti ochepa chabe. Abrahamu anapeza chilumikizano chopatulika chimenecho mwathunthu, mwawona, iye anali nacho chinthu chonsecho palimodzi. Iye anazitcha zinthu, motsutsana ndi chikhulupiriro chake, ngati kuti panalibepo; ndipo anachita pa mfundo yomweyo. Ine ndikukhoza kulingalira, patapita pafupifupi zaka makumi awiri, winawake anabwera apo ndipo anati, “Tate wa mafuko? Huh! Abram, iwe unati dzina lako linali ‘Abrahamu,’ kutanthauza *tate wa mafuko*. Nanga uli ndi ana angati panopa, Abrahamu?” Mukuwona?

²¹⁹ Izo sizinamukhumudwitse iye mpang’ono pomwe. Baibulo linati, “Iye sanadzandime pa Mawu a Mulungu, kupyolera mu kusakhulupirira.” Iye anapita patsogolo pomwe akukonzekera, kusunga nsapato zonse ndi matewera ndi chirichonse, iye anali woti “adzakhala ndi mwana.” Ndizo zonse.

²²⁰ Ngakhale Sara anati, “Inu mukudziwa chimene chiti chichitike? Inu mudzakhala ndi mwana, koma ine ndikukuuzani inu momwe ife titachitire izo. Hagara tsopano ndi mdzakazi wanga, ine ndimpereka kwa iwe.” Chifukwa, mitala inali yololedwa nthawi imeneyo. “Ndipo iye adzakhala ndi mwana, ndipo ine ndidzamutenga mwanayo inemwini.” Koma

Abrahamu sanakhulupirire zimenezo. Ayi, iye sakanati achite izo. Koma Sara anadzozedwa kuti achite zimenezo.

221 Kotero, Mulungu anamuza Abrahamu, “Tiye nazo ndipo umumvetsere iye,” koma Iye anati, “komabe ichi si chimene Ine ndinakulonjezani inu. Iyi si njira yomwe Ine ndinalonjezera izo.”

222 Tsopano tawonani, iye anatcha chirichonse “motsutsana,” ndipo thupi lake pamenepo litafa, ndi mimba ya Sara chimodzimidzi. Tsopano, iye anali bambo wachikulire, usinkhu wa zaka handiredi. Sara anali ndi zaka nainte. Tsopano zindikirani! Kufa kwa mimba ya Sara kapena kufa kwa thupi lake sikunaganiziridwe nkomwe.

223 Mvetserani ku ichi.

Pakuti lonjezo, lakuti iye adzakhala wolowa wa dziko lapansi, silinaperekedwa kwa Abrahamu, kapena kwa mbewu yake, kudzera mu chilamulo, koma kudzera mu chilungamo cha chikhulupiro.

Pakuti ngati kukanakhala mwa lamulo . . . kukanakhala mwa lamulo kukhala wolowa, chikhulupiro chapangidwa kukhala chopanda pake, ndipo lonjezo liri . . . lopanda mphamvu:

Pakuti lamulo lichita mkwiyo: ndipo pamene palibe lamulo, palibe kulakwa.

224 Mvetserani kwa ichi, tsopano.

Amene motsutsana ndi chiyembekezo . . .

“Motsutsana ndi chiyembekezo,” ziyembekezo zonse zinali zitapita! O, nthawi iliyonse ine ndikayamba kumverera pang’ono “wokhumudwa,” apa pali mutu umene ine ndimatembenezirako, Aroma 4, mwawona.

(Monga kwalembedwa, Ine ndakupanga iwe kukhala tate wa . . . mafuko,) pamaso pa iye amene anamkhulupirira, ngakhale Mulungu, amene amafulumizitsa akufa, ndipo anazitcha zinthu zomwe kunalibe ngati kuti zinaliko. (“Mulungu ananena chomwecho!” Mukuwona?)

Amene motsutsana ndi chiyembekezo anakhulupirira mu chiyembekezo, kuti iye akakhale tate wa . . . mafuko; molingana ndi icho chimene chinayankhulidwa, Momwemonso idzakhala mbewu yako.

225 Tsopano mvetserani, ndime ya 19.

Ndipo posakhala wofooka mu chikhulupiro, iye sanaganizire thupi lake lomwe linali lakufa, pamene iye anali pafupifupi zaka handiredi, ngakhalenso . . . kufa kwa mimba ya Sara:

Iye sanadzandime pa lonjezo la Mulungu kudzera mu kusakhulupirira; koma anali wamphamvu . . . kupereka ulemereero kwa Mulungu;

226 Pa usinkhu wazaka handiredi? Tawonani, thupi lake tsopano lakufa (umuna wake), ndipo mimba ya Sarah yakufa. Iye ndi . . . Izo sizinkaganiziridwa nkomwe, pamene izo zinawululidwa kwa iye. Bedi limenero silimaganiziridwa. Ndiwe wolumala, kapena chirichonse chomwe iwe uli, sichimaganiziridwa. Chikukucho sichimaganiziridwa, kwa mnyamata wamng'onoyo. Akhoza kukhala wopuwala, chirichonse chimene chiri (ine sindikudziwa), izo sizimaganiziridwa. Musati muziganizire nkomwe izo.

227 “Koma dokotala anati, ‘Iye sadzachokapo konse pamenepa.’ Dokotala anati, ‘Iye sadzabweranso.’” Izo sizimaganiziridwa nkomwe.

228 “Chabwino, tawonani, ndine munthu wokalamba, ndikufika usinkhu wa zaka zapakati.” Nzosaganiziridwa nkomwe.

229 Ndipo ife ndife ana a Abrahamu (Aleluya!), osati monga Isaki analiri, koma Mbewu yake Yachifumu (kudzera mwa Yesu Khristu) mwa chikhulupiriro chimene iye anali nacho, Mbewu ya Abrahamu ikubwera mu masiku otsiriza kudzawala ngati nyenyezi. Ana a Abrahamu! “Sanaganizire thupi lake lomwe tsopano linali lakufa.” Ngakhale sanaganizirepo izo! Izo sizinabweretse ngakhale kukayikira ngati Mulungu akanachita izo kapena ayi, Mulungu anati Iye akanadzachita izo! Chifukwa chiyani? Izo zinawululidwa kwa iye. Ndi kulondola uko?

230 Pamene izo zawululidwa kwa inu, pamene izo kwenikweni . . . chinachake . . . Inu simungakhoze kuzipanga izo kuti zichitike, izo ziyenera kuti ziwululidwe kwa inu. Ndiye inu simuganiziranso nkomwe china chirichonse: kodi izo nzosatheka bwanji, simumaganizira zomwe adokotala ananena, inu simumaganizira zomwe amayi ananena, zomwe abambo ananena, zomwe mlaliki ananena, zomwe wina aliyense ananena. Inu mumangoganizira zomwe Mulungu ananena!

231 “Iye sanaganizire thupi lake lomwe tsopano linali litafa, ngakhaleenso kufa kwa mimba ya Sara.” Izo sizinabweretsetse ngakhale pansu pa kuganiziridwa. O, mai, izo zimangondigwedeza ine. Thupi lakufa, kapena kufa kwa Sara, mimba, sizinaganiziridwe pansu pa kuganiziridwa nkomwe.

232 Palibe zochitika zomwe zidzaganiziridwe pamene chikhulupiriro chapeza malo ake obzalidwapo! Pamene kachidutswa ka nyongolotsi kochokera kwa mwamuna kapeza—dzira mwa mkazi, ndipo onse a iwo achonde, chinachake chichitika. Aleluya! Adokotala akhoza kunena, “Inu simudzakhala ndi mwana. Ine ndikhoza kutsimikizira kuti zanu—nyongolotsi zanu ndi zakufa m’thupi mwanu, ndipo

mazira ake sadzakhala konse achonde.” Koma mulole dzira lachonde ilo, mulole nyongolosi imeneyo idzikankhire yokha ku dzira limenero nthawi ina, penyani chimene chiti chichitike; mnyamata wamng’ono uyo kapena msungwana wamng’ono uyo amabwera powonekera. Chifukwa chiyani? Chikhulupiriro chapeza malo ake obzalidwapo. Ntchito zimapita kukagwira ntchito, khungu pamwamba pa khungu, ndipo apa pamabwera kamunthu kakang’onoko. Ameni. Mulungu, tichitireni chifundo ife. O Mulungu, ngati ife tikanakhala Akhristu okhakhala monga ife tikuyenera kukhalira; ngati ife tikanakhala amuna ndi akazi omwe akanakhoza kumutenga Mulungu pa Mawu Ake! Inu simungathe kuchita izo mpaka zitawululidwa kwa inu.

Ine ndikuyenera kuti ndifulumire.

²³³ Zindikirani, chikhulupiriro choyera cha Mulungu chinalumikizidwa ndi ntchito zopatulika za mneneri Wake. Kumbukirani, chikhulupiriro choyera cha Mulungu chinawululidwa kwa Abrahamu. Iye anachilandira icho, ndipo pofika pamenepo iye anayamba ndi ntchito zake zopatulika, mwa kukhulupirira. Mbewu ya lonjezo inali ndi malo oti ikule. Bwanji ngati iye akanati (Abrahamu) “Chabwino, inu mukudziwa, Sara, ndiponso, izo zakhala zaka twente faivi kuchokera pamene Mulungu anapanga lonjezo limenero”? U-o! “Ngati chinachake chikanati chichitike,” mwawona. Koma izo sizikanatero. Mulungu ankadziwa kuti sizikanatero.

²³⁴ Bwanji ngati namwali Mariya akanati, “Chabwino, tsopano, dikirani miniti! A—namwali kuima? Chabwino, iwo anditulutsa ine mu mpingo wanga ngati ine nditi ndilowe umo ndi kunena chinthu chotero monga icho”? Tsopano, iye akanaganiza maganizo amenewo ngati iyo ikanapanda kukhala nthaka yobzalirapo yokonzedwa.

²³⁵ Pamene mneneri uja anati, “Namwali adzaima,” izo zinakhazikitsa icho. Mukuwona?

²³⁶ “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Ngati nthaka yobzalirapo ili pamenepo pamene Mawu amenewo agwera pamenepo, Iyo imagwiritsitsa. Palibe chinthu chimene chingakhoze kuimitsa Iyo.

²³⁷ Tsopano, mwamsanga, pamene ife tikutsiriza. Mwawona, Mbewuyo inali nawo malo obisalapo. Mulungu ankadziwa izo, apo ayi Iye sakanapereka lonjezolo kwa Abrahamu. Tsopano, mvetserani mwatcheru kwenikweni tsopano. Mulungu ankadziwa kumene lonjezo limenero linkapita; Iye sanamuyitane nkomwe Abrahamu mpaka iye atakwanitsa usinkhu wazaka sevente faivi, koma iye anali wantchito Wake wokonzedweratu kuchokera pachiyambi, chomwechonso anali Sara.

²³⁸ Zindikirani, kumbukirani, iye analibe Baibulo loti aziwerengamo. Iye analibe izo mophweka monga ife tiri nazo

izo lero, kuti tiziwerenga Mawu Ake ndi kuwona ena amene anawatenga Iwo. Kumbukirani, iye anali nawo Iwo kokha mwa vumbulutso, ndipo ndicho chinthu chenicheni. Chimodzimodzi monga izo zinali ndi Yosefe, mu Genesis, kunalibe Baibulo. Kumbukirani, Mose analemba Genesis, Eksodo, Levitiko, ndi Deuteronomo. Palibe aliyense wa anthu amenewo amene anali ndi Baibulo lililonse loti aliwerenge kufikira pambuyo pa Mose. Ndi kulondola uko? Iwo analibe Baibulo limene ife tiri nalo, kuti litithandize ife mu chikhalidwe chatu cholumala. Iwo anali amuna olimba amene. . . zinawululidwa kwa iwo ndi Mulungu, ndipo iwo anayima pamenepo. Panalibe chomwe chinawasuntha iwo. Tsopano, kodi inu mukuganiza kuti ife tingakhozebe kukhala nacho chikhulupiriro cholimba icho? Ngati Izo zawululidwa kwa inu!

²³⁹ Mukhululukire kufotokozako, kapena umboni pa nthawi ino, basi tisanatseke. Ine ndikukumbukira izo kuno mu “Twin City,” ine ndikuganiza M’bale Brown ndi iwo anali ndi ine; ndipo ine ndinali kutenga moyo wa Yosefe, mu Baibulo. Ndipo ine ndinawerenga Baibulo limenero, panali munthu amene analibe kanthu kotsutsa! Abrahamu, Isaki, Yakobo, ndi onse a iwo, anali ndi chinachake chowatsutsa iwo, koma osati Yosefe. Munthu wotani, munthu wangwiwo, choyimira changwiwo cha Khristu!

²⁴⁰ Pamene ine ndinawerenga zimenezo, ine ndinangoyamba kulira, tsiku lina, mu chipinda changa chaching’ono chakale cha hotelo. Ndipo ine ndinapita mu chipinda momwe ine ndinali nazo zovala zanga zitapachikika, ndinakokera chitseko palimodzi, ndipo ine ndinati, “Mulungu, ine ndikufuna kuti ndikuthokozeni Inu chifukwa cha munthu ngati Yosefe, munthu amene anayamba wakhala pa dziko lapansi, mu—munthu muthupi monga ine ndiliri, munthu yemwe anakhoza kukukhulupirirani Inu ndi kutenga Mawu Anu.” Iye ankadedwa ndi abale ake. Iye sakanatha kudziletsa kukhala wauzimu. Iye ankawona masomphenya. Iye amakhoza kutanthauzira maloto. Onse a iwo ankamuda iye chifukwa cha izo. Iye sakanachitira mwina, ndicho basi chimene iye anali.

²⁴¹ Mwawona, izo sizinali kwa ena basi. Iwo ankayenera kuti azimukonda iye, koma mmalo mwa izo. . . Pamene iye anawauza iwo, nthawi zina zinthu zotsutsana nawo, “O,” iwo amati, “apa pakubwera wolota uja.” Mukuwona? Ndipo iwo anamuda iye popanda chifukwa.

²⁴² Ine ndinati, “Nchifukwa chiyani iwo anachita zimenezo?” Ndipo komabe mwamuna ameneyo sanasunthike konse, iye anakhala pomwepo. Mwawona? Ine ndinati, “Zikomo Inu, Ambuye. O Mulungu, zikomo Inu chifukwa cha munthu woteroyo.”

²⁴³ Ndipo pomwepo Mzimu Woyera unawululira kwa ine, unati, “Udzakhala ndi mwana wamwamuna, ndipo udzamutcha dzina

lake ‘Joseph.’” Ine ndinanyamuka kuchokera pamenepo ndipo ndinathokoza Ambuye.

244 Becky, wakhala kumbuyo uko, anali atangobadwa kumene pafupifupi. . . iye anali pafupifupi chaka chimodzi. Iye anali wa opareshoni, izo zimayenda m’banja la mkazi wanga kukhala wa opareshoni; chifukwa iwo samamasuka monga momwe mkazi amayenera kuchitira, mafupa ndi olimba ngati mwamuna, ndipo iye anachita kudulidwa kuchoka kwa amayi ake. Ndipo adokotala anandiuza ine, “M’bale Branham, musati mudzakhale ndi mwana wina ndi mkazi uyu.” Anati, “Chiberekero chake ndi chopyapyala ngati baluni.” Iye anati, “Kulibwino mundilole ine ndimange machubu amenewo.”

245 Ine ndinati, “Ayi, sindikanatero. . . musati muganize zochita zimenezo, ‘Adokotala.’”

246 Iye anati, “Chabwino, inu—inu—inu. . . Iye sakuyenera kudzakhala ndi mwana wina.” Anati, “Inu mudzamuwononga iye,” anati, “iye adzafa.” Anati, “Ife tinali ndi nthawi yoyipa kumeneko,” anati, “inu basi. . . iye anali anangodutsamo kumene.”

247 Ndipo kenako Ambuye anandiuza ine “ndidzakhala ndi mwana wamwamuna” ndipo dzina lake lidzatchedwa “Joseph.” Ine sindinachite mantha nazo izo. Nonse, ambiri a inu, mukukumbukira.

248 Ine ndinapita, kumalengeza izo, “Ine ndidzakhala ndi mwana; dzina lake adzakhala Joseph.” Ndi angati amene akukumbukira izo? Ndithudi! Konse kuzungulira, kudziko lonse, kulikonse, nkumawauza anthu, “Ndidzakhala ndi mwana; dzina lake lidzakhala Joseph.”

249 Chimodzimodzi basi monga mnyamata wamng’ono uja anaukitsidwa, mu Finland, kwa akufa. M’bale Jack anali pomwepo pamene izo zinkachitika. Ndinakuuzani inu, zaka ziwiri kapena zitatu izo zisanachitike, “Padzakhala mnyamata wamng’ono,” momwe iye adzavalire, pamene iye adzagone. “Mulungu ananena chomwecho!”

250 “Kodi izo zikhala motani?”

251 “Ine sindikudziwa! Koma izo zinawululidwa kwa ine kuti izo zikanadzachitika!”

252 Izo zinawululidwa kwa ine, “Ine ndinali kupita ku Arizona, ndipo kumeneko ine ndikanakakumana ndi Angelo seveni. Ndipo iwo amakhoza kundiuza ine, ndipo, o, Uthenga umene ine ndimayenera kuwulalikira.” Ndipo izo zinali Zisindikizo Seveni. Izo zinachitika! Ndi angati akukumbukira ine ndikunena zimenezo? Matepi ndi zinthu zinajambula zimenezo. Ndipo izo zinachitika! Magazini, china chirichonsecho, zinatenga chithunzi cha Izo. Kuwala kumeneko m’mlengalenga, iwo sangakhoze nkomwe kukumvetsa Iko. Apo izo zinali.

253 Ine ndikukumbukira ndikumuyitana M'bale Jack ndi kumufunsa iye za izo, Khristu pokhala atayima pamenepo, ndipo M'bale Jack anati, "Zimenezo ziri mu chikhalidwe Chake cha ulemerero." Mukuwona? Ine ndimamukonda M'bale Jack. Iye ndi mmodzi wa a fiyoloje opambana omwe ine ndikuwadziwa, koma ine sindikanakhoza basi kuzigunda izo molondola basi.

254 Ine ndinali kuyima pamenepo, ine ndinati, "Ambuye, Mnyamata uyu wapezeka bwanji pano," ine ndinati, "ndi tsitsi ngati ubweya?"

255 Ndipo Iye anati, "Iye ali ndi wigi." Penyani mu bukhu, izo zisanachitike nkomwe, ine ndinazinena izo. Ndipo tsiku limenero pamene izo zinachitika, Iko kunakwera mmwamba. Ndipo kenako inu mutembenezire chithunzicho cham'mbali, ngati inu muli ndi *Look* Magazini kapena *Life* Magazini, tembenziranani cham'mbali. Ndi Uyo apo, mwangwiro basi, *Mutu wa Khristu wa Hofmann*, akuyang'ana pansu pomwe ine ndinali kuyima; apo Izo ziri mu magazini! Ndi angati anaziwonapo Izo? Ndithudi, inu nonse mwaziwona. Pamenepo, kuyang'ana mmbuyo momwe, zinatsimikizira ndendende kuti vumbulutsolo linali lolondola.

256 Nchifukwa chiyani anavala wigi? Bwanji, oweruza akale Achingerezi, oweruza Achiyuda, anakakonda kuvala wi—wi—wigi, iwo amazichitabe ku England; pamene iye... umenewo ndi ulamuliro wapamwamba, iye amavala wigi. Ndipo izo zinamuwonetsa Iye atayima pamenepo, atavekedwa wigi ndi mapiko a Angelo, Iye ndi Alefa ndi Omega. Iye ndi Woweruza Wamkulu, ndipo palibe wina koma Iye. Iye ayenera kuyang'anidwa ngati Alefa ndi Omega. Ndipo apo Iye anali Mnyamata, ayi, kapena kupitirira, usinkhu wa zaka sarte, atavala wigi yoyera. Kuwonetsa kuti Iye anali Wapamwamba, Mulungu, "Atate apereka chiweruzo *chonse* m'manja mwa Mwana." Aleluya! Vumbulutsu sililakwika konse! Liyankhuleni Ilo mulimonse, ziribe kanthu momwe izo zikumvekera ngati, zimayenda molondola ndi Mawu.

Ndipo ine ndikukumbukira, zaka zinayi patsogolo pake, mkazi wanga...

257 Ife tinkadziwa kuti ife tikhala ndi mwana. Aliyense anati, "Kodi uyu ndi Joseph akubwera?"

258 Ine ndinati, "Ine ndikuganiza ndi choncho, ine sindikudziwa, koma ine ndidzakhala ndi Joseph."

259 Pamene iye anabadwa, uyo anali Sara. Kenako munthu anandiitana ine, ndipo anaseka pamaso panga, iye anati, "Anati, inu mukudziwa chiyani? Inu mumatanthauza Josephine!" (Munthuyo anafa. Munthuyo anafa.)

260 Ine ndinati, “Bwana ine ndinati, ‘Mulungu anandiuza ine ine “ndidzakhala ndi mwana wamwamuna” ndipo ine ndidza “mutchula dzina lake ‘Joseph’!””

261 Panali anthu atatu amene anachoka ku mpingo wina wachipembedzo ndi kubwera ku mpingo wathu, ndipo anandimva ine ndikunena izo. Pamene Sara anabadwa, iwo anati, “Huh! Iye ndi mneneri wabodza.”

262 Ine ndinati, “Dikirani miniti, madona, ine sindinanene kuti *liti*, ngakhale Mulungu sananene kuti *liti*. Iye anandiuza ine, ndi ‘dzakhala ndi . . .’ Iye anali . . . anamuuza Abrahamu, iwo ‘adzakhala ndi Isaki,’ koma Ishmaeli anabadwa pakati pa nthawi imeneyo, koma izo sizinachotse Izo.” Ine ndinati, “Mulungu anati ine ndidzakhala ndi mnyamata uyu ndipo iye adzamutcha dzina lake ‘Joseph.’”

263 Adokotala anati, pamene iye anabwera, iye anati, “Abusa, ine ndimanga machubu amenewo tsopano.” Anati, “Ine . . .”

264 Ine ndinati, “Musati muchite zimenezo!” Ine ndinati . . .

265 Iye anati, “Chabwino, inu mukhoza kukwatiranso ndi kudzakhala naye mnyamata ameneyo apobe.”

266 Ine ndinati, “Ine ndidzakhala naye ndi iye! Mulungu ananena chomwecho!” Ine sindikanakhoza kuziwerenga izo kuchokera mu Baibulo koma izo zinalembedwa pa mtima wanga mwa vumbulutso, mwa chikhulupiriro; Mulungu ananena chomwecho! Sindinafune kuti ndidzandime pa lonjezo la Mulungu kudzera mu kusakhulupirira.

Ena a iwo anati, “Inu mumatanthauza ‘Josephine.’”

Ine ndinati, “Ine ndimatanthauza ‘Joseph.’”

Adokotala anati, “Iye sangakhale ndi mwana wina.”

Ine ndinati, “Iye adzakhala ndi mwana wina.”

267 Zaka zinayi zinadutsa, potsirizira iye anali woti akhalanso mayi kachiwiri.

268 Kenako mkazi, (uneneri wabodza wotumizidwa ku dziko lonse) akulemba mawu, anati, “Tsopano Meda adzafa, mu nthawi iyi, chifukwa ine ndinatimizidwa kuti ndidzamtsozogolere Bill.” Ndipo ilo linanena kuti “Iye sandimvera ine chifukwa ndine mkazi, ndipo Mulungu amubwezera iye tsopano pakupha mkazi wake.”

269 Ine ndinati, “Mulungu anatumiza Yesu Khristu kuti adzanditsogolere ine.” Mwawona? Ndipo ine ndinati, “Ine ndimatsozozedwa ndi Mzimu.”

270 Meda wamng’ono wosauka. Ife tinali naye namwino yemwe anali atachiritsidwa kumeneko mmisonkhano, inu nonse mukuwadziwa Akazi a Morgan, ndi mmodzi wa anamwino a Mayos, vuto lalikulu la . . . chabwino, iye ali mu mbiri, “wakufa,” pafupifupi zaka twente zapitazo, ndi khansa, “khansa ya

sarcoma,” ku Louisville, pomwepo pa mbiri ya chipatala cha Baptisti. Iye akugwira ntchito mu—mu Jeffersonville, mu chipatala, tsopano. Iye wakhala ali kumeneko kwa zaka zonse izi, chifukwa Mulungu anati “Iye adzakhala moyo.”

271 Ndipo, kotero, Meda anamukonda iye, ndipo iye anati, “Ine ndikufuna Margie abwere nane, Bill, ine sindikumverera ngati ndipita ku chipatala.”

272 Ine ndinati, “Usati upange...Ife timamukonda Margie, koma Margie si Mulungu wathu, Margie ndi mlongo wathu.” Ndipo ndinanyamuka kupita ku Green’s Mill. Iye anandiskonezeratu ine. Ndithudi, ine ndimamukonda iye. Ndipo ine ndinapita ku Green’s Mill.

273 Ndipo iye anati, “Bill, kodi iwe ukuganiza kuti ine ndifa?”

274 Ndipo ine ndinati, “Ine sindikudziwa, koma mwanayo abadwa, mulimonse. Iwe udzakhala naye Joseph.”

275 Iye anati, “Kodi uyu ndi iyeyu?”

276 Ine ndinati, “Ine sindikudziwa, Wokondedwa. Ine sindingakhoze kunena, koma Mulungu anati iye ‘akhala naye Joseph,’ ndipo ife tikhala naye Joseph. Ine sindikusamala chimene chirichonse chikunena, ife tikhala naye Joseph. Pakuti, Mulungu yemweyo amene wandiuzwa ine mavumbulutso onse awa, anandiuzwa ine *zimenezo*, Iye sanalepherepo pa zina ndipo Iye sadzalephera pa *zimenezo*.”

277 Ine ndinapita pamwamba, pa chigayo, kuti ndikapemphere. Ndipo ine ndinayamba kumeneko. Apo panayima Kuwala kuja kukulendewera pakati pa mitengo iwiri, kunati, “Bwerera ku lako, kunali, ku Bukhu.” Ine ndinabwerera ku—Baibulo, ndipo pamene ilo, ndipo ilo linakhala liri mu galimoto yanga, ndipo pamene ilo linatero, mphepo inali itauluzira ilo pamene Natani anali atakhala, ndi Davide, anati, “Pita ukamuwuze mtumiki Manga Davide, Ine ndinamtenga iye ku khola lankhosa lija, kuchoka koweta nkhosa zowerengeka za atate ake, ndipo Ine ndinampangira dzina lalikulu ngati amuna aakulu.” (Osati zonse—dzina lalikulu kwambiri, koma *monga* amuna aakulu; sanamupange konse iye Billy Graham, koma a...kumupatsa iye dzina, inu mukudziwa.) Anati, “Ine ndinachita *zimenezo*, koma,” anati, “Ine sindingamulole kuti iye amange kachisi, koma mwana wake...”

278 Ndipo mwamsanga pamene Ilo linati, “mwana Wake,” o, mai, izo zinali pamenepo.

279 Ine ndinati, “Joseph?” Ndiko kulondola.

280 Kumusi komwe kunyumba ine ndinapita. Ndipo apo, mwana wamng’onyo, wamkulu kwambiri, iye anka-... (mnyamata wakale wamkulu) iye sankatha kuyenda, akudutsa mmunda. Ine ndinathamanga, ndinaponyera mikono yanga momukumbatira

iyе, ndipo ine ndinati, “Wokondedwa! Joseph akubwera. Joseph ali panjira yake.”

²⁸¹ Aliyense akudziwa, ndi oparesoni, inu simungalole kuti mwana atsike. Usiku umenewo mwanayo anatsika, madzi anaphulika, china chirichonse.

²⁸² Mmawa wotsatira, m’ma seveni koloko, ife tinapita ku chipatala, adokotala anati, “O, chifundo, ubwino.”

²⁸³ Ine ndinamupsopsona iye kumutsanzika, ndinati, “Wokondedwa, sipatenga nthawi, Joseph akhala ali pano.” Mmwamba mmasitepe iye anapita, monga choncho, pa tebulo la oparesoni.

²⁸⁴ Mphindi zocheпа, namwino anatsika, anati, “Abusa a Branham?”

²⁸⁵ Ine ndinati, “Inde, mayi.”

²⁸⁶ Iye anati, “Inu muli ndi wabwino, wamapaundi seveni, ma aunsi atatu, mnyamata.”

²⁸⁷ Ine ndinati, “Joseph, mwana, walandiridwa.” Inde, bwana! Chifukwa chiyani? Chifukwa chiyani? Ndi chiyani icho? Izo sizinalembedwe mu Baibulo kuti zikanadzachitika, koma Mulungu yemweyo wa Baibulo amene anawulula izo kwa Abrahamu, ife sitinaganizire kufa kwa mimba yake, kusatheka kokhala mwanjira imeneyo. Inu simumadzandima pa lonjezo la Mulungu kudzera mu kusakhulupirira, koma inu mumapereka matamando kwa Mulungu, kudziwa kuti izo ziyenera kuti zichitike! Ine sikundisamala zomwe adokotala akunena, china chirichonse chimabwera mwanjira iliyonse, koma inu musati mukhulupirire izo, ndi bodza la mdierekezi. Inde, bwana, zowona. Chikhulupiro chimapita paliponse, limodzi ndi ntchito, kuti chilenge lonjezo. (Tiyeni tifulumire.)

²⁸⁸ Ndendende basi, akuti apa, “Rahabu hule,” Yakobo anati, “analongamitsidwa ndi ntchito.” Koma chifukwa chiyani? Chikhulupiriro chake!

²⁸⁹ Iye anati, “Ine ndikumva kuti Mulungu ali ndi inu.” Iye sanafune kuwona momwe Yoswa anakonzera tsitsi lake, kapena momwe iye anavalira zovala zake. Iye anati, “Ine ndikudziwa kuti Mulungu ali ndi inu.” Ndizo zonse zomwe zinali zofunika, iye anakonzekera.

²⁹⁰ Monga masomphenya owona lero, (ine ndikutseka mu kamphindi chabe) masomphenya owona ochokera kwa Mulungu lero, ndi Mawu olonjezedwa a tsikuli. Mukuti, “Masomphenya awa, M’bale Branham, inu mukuzitenga kuti izo?” Anthu amapunthwa pa zimenezo. Kodi Machitidwe 2:17 sanati, “Zidzachitika mmasiku otsiriza kuti anyamata anu adzaona masomphenya, ndipo aakulu anu adzalota maloto”? Sikulondola uko? Ndicho chimene Baibulo linanena.

291 Chabwino, tsopano ngati izo ziri chomwecho, yang'ananso pa Malaki, mutu wa 4, ndi kupeza ngati izi sizinalonjezedwe lero. Inu mungakhoze bwanji kukhala nacho chikhulupiriro mwa Iwo? Baibulo linanena chomwecho!

292 Tsopano inu mutenge Luka 17:30 ndi kuwerenga izo. Yesu anati, "Monga izo zinaliri mmasiku a Sodomu, momwemonso izo zidzakhala ziri mu kudza kwa Mwana wa munthu." Monga momwe izo zinaliri ku Sodomu. Tsopano, tayang'anani pamene dziko liri lero: Achisodomu. Tayang'anani pa Billy Graham ameneyo ndi Oral Roberts, mboni ziwiri izo, kumusi uko akuchitira umboni kwa mipingo ya zipembedzo. Mmodzi kwa Amethodisti, Abaptisti, ndi Apresbateria; winayo kwa Achipentekoste. Chimodzi *Ichi*, chimodzi *icho*, ndi chimodzi *chinacho*.

293 Koma kumbukirani, Abrahamu sanali mu Sodomu, iye anali atayitanidwa kale kutuluka. Ndipo apo panali Mmodzi amene anatsalira ndipo ankayankhula kwa iye! Ndipo Amene anakhala ndi kuyankhulana naye, anamuwonetsa *iy*e chizindikiro. Ndi nsana Wake utatembenezidwa, Iye anati Sara adzakhala ndi mwana amene iye anali atamuyembekezera. Amen. Ndi nsana Wake utatembenezidwa. Ndipo iye anamutcha Iye, "Mulungu, Elohim."

294 Tsopano, izo zikufika pochitika lero, chifukwa ife tiri nacho chikhulupiriro. Ndipo ine ndikudziwa izi ndi za Mulungu, ndi chifukwa chakuti ichi ndi Malemba ena akuloza ku ora lino. Chivumbulutso 10 amanena kuti "mu ora la Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, pamene iye ayamba kuwomba Uthenga wake," osati mu msonkhano wa machiritso, koma Uthenga umene umatsatira msonkhano wa machiritso.

295 Yesu anapita ndipo analalikira. Iye anati, "Iye anachiritsa odwala, ndi chirichonse. O, Rabbi wamng'ono ameneyo, Mneneri, Iye ndi Munthu wamkulu. Ife tikumufuna Iye mu mpingo wathu."

296 Koma tsiku lina Iye anayimirira, anati, "Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi." O, mai. Iwo sanamufunenso Iye pamenepo. Inde. O!

297 "Pokhapokha inu mutadya thupi la Mwana wa munthu, ndi kumwa Magazi Ake!" Iye sanafotokoze Izo. Anati, "Pokhapokha inu mutadya thupi la Mwana wa munthu, ndi kumwa magazi Ake, inu mulibe Moyo mwa inu."

298 Bwanji, ine ndikuganiza, madokotala ndi anamwino ena anati, "Munthu uyu ndi mthakati, akuyesera kutipangitsa ife kuti tizimwa magazi ake." Mwawona, iwo sanazimvetse Izo. Iye ankadziwa izo.

299 Koma ophunzira awo, iwo mwina sakanatha kuzifotokoza izo, koma iwo anakhala pamenepo ndipo anawakhulupirira Izo

mulimonse, ameni, pakuti Izo zinawululidwa kwa iwo. Inde, bwana. Iwo ankadziwa Izo, Malemba anali atafotokoza Izo.

³⁰⁰ Izo zikanakhoza kufunsidwa ndiye kwa ine za izi, ngati inu munganene, “Chifukwa chiyani inu muli ndi chikhulupiriro kuti mukhulupirire masomphenya awa, pamene—pamene pali zotsanzira zambiri zabodza zikuchitika?”

³⁰¹ Ine ndiyankhula chinachake chaching’ono, cholimba, kwa miniti yokha tsopano. Pamene zotsanzira zabodza zambiri ziri mozungulira, kumbukirani, m’bale wanga, izo zanenedwanso kuti izo ziyenera kukhala ziri pano pa nthawi yomwe ino. Ndizo ndendende, monga zinaliri mu nthawi za Mose. Mose anapita uko kukachita ntchito za Mulungu pamaso pa anthu, ndipo apo panali Yambre ndi Yane atayima pamene. Koma ndani anali woyamba kuchita zimenezo? Ndiye ena awa anali otsanzira, chifukwa pankayenera kuti pakhale chapachiyambi poyamba kuti iwo achitsanzire. Ngati iwo akanakhala apachiyambi. . . U-nhu. Ayi, ife sitina—ife sitinatayike. Ife tikudziwa pamene ife tiri, mwawona, mwawona, mwa Lemba ndi mwa vumbulutso la Mulungu. Ndi chifukwa chake inu mukuyimabe.

³⁰² “Bwanji, munthu *uyu*, iye amawona masomphenya ndi zina zotero. Iye amachita *izi*, ndipo iye amathamanga mozungulira ndi mkazi wa mwamuna *uyu*. Iye amakhulupirira mwa—mwa milungu itatu, ndi zinthu zonse *izi*.” Izo sizimadzandimitse Izo mpang’ono pomwe. Ndipo apa pali chinthu chimodzi chimene iwo sangakhoze kuchitsanzira: Mawu! Zindikirani. Iwo akhoza kukhala nazo zinthu zonse *izi*, iwo akhoza kuyankhula mmalirime, iwo akhoza kufuula, kuvina mu Mzimu, ndipo nkukhalabe adierekezi. U-nhu. Uko nkulondola. Uko nkulondola. Koma Mawu awa amawayeza iwo. Mukuwona? Ndizo ndendende zolondola. Apa ndi pamene izo zimafika. Monga Mose, ndi Yambre. . .

Ndipo kumbukirani, Iye anati, “Monga Yambre ndi Yane anatsutsana ndi Mose, mmasiku otsiriza otsanzira awa adzadzukanso pa dziko lapansi.” Kodi Iye anazinena izo? Chabwino, ife tiri nawo iwo.

³⁰³ Koma zimenezo sizinamudzandimitse Mose. Pamene Mose anatembenuka ndi kuchita chozizwitsa mu Dzina la Ambuye, ndipo apa panayima otsanzira awa, anachita chinthu chomwecho. Izo sizinamuletse iye, kuti, “Chabwino, ine ndikuganiza kulibwino ine ndizisiye ndi kuchoka ku mundawu.” Iye anakhala pomwepo. Za chiyani? Izo zinawululidwa kwa iye. Aleluya! Iye ankadziwa mwa Mawu a Mulungu. Iye ankadziwa kuti Mawu potsiriza akanadzawagwira iwo. Iye ankadziwa kuti ikanadzafika nthawi imene Mawu akanadzaziwonetsera Okha, ndipo iwo sakanakhoza kupita patsogolo ayi.

³⁰⁴ Kotero ine ndazidziwa *izi*, zaka zonse *izi*, mwawona, ndiko kulondola, kuti nthawiyo ikanadzafika. Pamene chozizwitsa

chirichonse, ngati Mulungu atumiza chozizwitsa chenicheni, nthawizonse pamakhala kusintha mu dongosolo lonselo. Ngati Mulungu atumiza chinachake mu mpingo, ndipo dongosolo lakale silinasinthe, Iye anachitumiza icho pachabe. Pamene uthenga ukupita mu zizindikiro ndi zodabwitsa, pali Uthenga umatsatira zimenezo. Pamene Yesu ankapita namachiritsa odwala, ndiye panadza Uthenga Wake, “Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi. Ine ndine Iye.” Mukuwona? Mwawona, iwo—iwo sanakhulupirire Zimenezo. Iwo anakhulupirira zozizwitsa Zake. Anati, “Ngati inu simungakhoze kundikhulupirira Ine, khulupirirani zozizwitsa izo, pakuti izo zimachitira umboni kwa inu, Yemwe Ine ndiri.” O, mai. Ulemerero! Ndani anali woyamba? Mose! Kenako iwo anamutsanzira iye. Koma zoonadi zazikulu zikadali chimodzimodzi, pakati pa cholondola ndi cholakwika, iwo sangawuvomereze Uthenga! Iwo sangakhoze kuvomereza Uthenga umene uli wosayipitsidwa, kuchoka ku Mawu a Mulungu.

³⁰⁵ Ine sindikusamala, Yudasi akanakhoza kuchita mitundu yonse ya zizindikiro ndi zodabwitsa; koma, pamene iye anabwera kuti adzalandire Mzimu Woyera pa Tsiku la Pentekoste, iye anawonetsera mawanga ake. Mdierekezi ameneyo akhoza kubwera apo ndi kutsanzira ku chinthu chomwecho, kufikira icho chitafika ku Mawu awa, koma iye sangakhoze kuwatenga Mawu onse amenewo. Iye akhoza kuzibweretsa izo zonse, mwinamwake ku Mawu amodzi monga Eva anachitira, mdierekezi anachitira kwa Eva, koma iye sangakhoze kuwoloka izo zonse. Chifukwa chokhacho... chinthu chonsecho ndi Thupi la Khristu. Mwawona, Mawu tsopano. Ngakhalenso sakanakhoza...Iwo sakanakhoza, sangatenge Uthenga tsopano, ngakhalenso Yambre ndi Yane sakanakhoza kutenga Uthenga wa Mose. Iwo sakanakhoza kuchita izo. Ntchito zawo zotsanzira zinadziwika, chifukwa iwo sakanakhoza kutsatira Mawu a Mulungu otsimikiziridwa ndi mneneri Wake wodzodzedwa. Mwawona?

³⁰⁶ Iwo sakanakhoza kutsatira Israeli kunjira. Chifukwa chiyani? Iwo anali achipembedzo, makanda a Aigupto, Iwo sakanakhoza kutsatira Mawu amenewo, Ngati iwo anatero, iwo akanayenera kuchoka ku Igupto, kukana zonse zinali zabwino kwa iwo, ndipo iwo sakanatha kuchita izo. Ngakhale iwo akanakhoza kutsanzira ntchitozo, ndi kuchita zimene Mose anachita, koma kupusa kwawo kunawonekera pamene inafika nthawi yoti achoke. Ndiye Mulungu anazitsanulira kwenikweni izo, pa iwo.

³⁰⁷ Chimodzimodzi tsopano! Iwo akhoza kuchita mitundu yonse ya zotsanzira zaboroda ndi zinthu, izo sizimachita kalikonse koma kumangokulitsa chinthu cholondolacho. Ndipo mwana wokhulupirira aliyense amadziwa kuti icho ndi Choonadi. U-nhu. Apa inu mukuwona mwa poyera, ndiye, ntchito za kupusa kwawo kwa kutsanzira kwawo. Ngati zanu—ngati

ntchito zanu ziri Mawu owona ndi zotsimikiziridwa ndi Iwo, ndi chikhulupiriro chanu, izo zidzawonekera ndipo... monga lonjezo la Mulungu, mu Mawu Ake olembedwa apachiyambi.

³⁰⁸ Yesu anati, “Ngati Ine sindichita ntchitozo...” Mvetserani mwatcheru! “Ngati Ine sindichita ntchitozo...” Ndiloleni ine ndiwonjezere izi kwa Izo. “Ndiko kuti, ngati Ine sindichita ntchito zimene Malemba amakuwuzani inu kuti Ine ndidzachita, ndiye...chitani izo mu m’badwo Wanga, pamene Ine ndidzabwera, chimene Mesiya ankayenera kuti adzachite pamene Iye adzabwera. Ngati zinthu zimene ine ndizichita, ngati Mulungu sawatsimikizira Mawu amenewo amene Iye ananena kuti akanadzachitika, ngati moyo Wanga sukuwapanga Mawu amenewo kukhala chimodzimodzi basi zomwe Iwo anati Iwo akanadzachita...” Musati muphonye izi! Yesu akuti, “Inu mukudziwa chimene Mesiya akuyenera kuchita. Ndiye, ngati Mawu amenewo amene alembedwa, ndiyeno Iwo samadziwonetsera Okha kudzera mwa Ine, ndiye ine sindine Iye.” Ameni! “Ndiye tsiku limene ine ndimakamba za ilo ndi lolakwika, zomwe Yohane ananena za Ine zinali zosawona. Ndiyeno ngati ine sindine Mesiya ameneyo, ngati ntchito izo zimene Mesiya ankayenera kuti adzazichite, Iye—Iye akuyenera kukhala, ‘Ambuye Mulungu wanu adzakudzutsirani mneneri wonga ine,’ ndipo inu simunakhale naye mneneri kwa zaka mahandiredi, ndipo ngati ntchito izo zimene Ine ndikuchita, zimene Mulungu analonjeza, ngati izo sizimawonetseredwa mmoyo Wanga wapanopa, ndiye Ine sindine Iye. Koma ngati Mawu olonjezedwa a m’badwo uno atsimikiziridwa mwa Ine, ndiye Ine ndine Iye ndipo lonjezo labwera kwa inu.” O, mai, sindikuwona momwe Izo zingakhalire zomveka bwino! “Ngati lonjezo siliri...” O!

³⁰⁹ “Ndiye ngati lonjezo la tsiku limenero likuwonetseredwa mu utumiki Wanga,” anatero Yesu, “ndiye Ine ndine Iye. Kotero ngati inu simungakhulupirire nkomwe yemwe Ine ndiri, ndiye yang’anani pa ntchito zimene zalonjezedwa za tsiku lino.” Ameni! “Tayang’anani pa ntchito zomwe zalonjezedwa. Ngati ntchito zimenezo sizinakwaniritsidwe, iliyonse ya izo mwa Ine, ndiye musati mundikhulupirire Ine, chifukwa Ine ndakuwuzani inu zolakwika. Inu simungakhoze kundikhulupirira Ine, ingoyang’anani chimene Baibulo linanena kuti zikanadzachitika mu tsiku lino. Ngati izo sizikuchitika, ndiye izo siziri zolondola. Ngati zinthu zabodza izi siziri pano, ndi zinthu zina zonse izi, ndi zinthu zomwe zikuyenera kuchitika; ngati izo siziri pano, ndiye ine ndikulakwitsa. Koma ngati izo ziri,” Yesu anati, “ndiye Ine ndine Iye.” Ameni! “Ine ndine Iye amene analonjezedwa kuti adzabwera.”

O, mai, ntchito zomwezo zimene zinalonjezedwa, mu tsiku Lake, zinamutsimikizira *Iye* kuti anali Mesiya ameneyo. Kodi inu simukukhulupirira zimenezo?

³¹⁰ Chabwino, tsopano, m'bale, ngati ntchito za Luka, mutu wa 17 ndi ndime ya 30, lonjezo la Yesu Khristu, basi kusanachitike kudza Kwake, kuti dziko likanadzabwerera ku Sodomu ndipo amithenga akanadzatuluka, ndipo zinthu zikanadzachitika ndendende basi; ngati izo sizikuchitika, ndiye musati mundikhulupirire ine kuti ndakuwuzani inu Choonadi. Koma ngati izo zikuchitika, ndiye khulupirirani kuti Ndi Iyeyo, "Mu tsiku limenero Mwana wa munthu adzawululidwa." Amen! Mwana wa munthu adzawululidwa mu thupi la nyama, inu anthu, Mpingo, ndendende basi monga mowme zinaliri asanafike masiku a Sodomu, gulu loyitanidwa kutuluka kuchoka kwa onse a iwo, atakhala kunjira, akukhulupirira lonjezo la Mulungu. Ulemerero!

³¹¹ Ndiye, ntchito zomwe Mzimu Woyera ukuchita lero, mwa masomphenya awa osalephera konse, malonjezo osalephera konse, zizindikiro zonse zautumwi zolonjezedwa mu Baibulo, za Malaki 4, ndi, o, Chivumbulutso 10:7, zonse za izo zikukwaniritsidwa; ndi kutsimikiziridwa mwasayansi, njira ina iliyonse. Ndipo ngati ine sindinakuwuzani inu Choonadi, zinthu izi sizikanati zichitike. Koma ngati ine ndakuwuzani inu Choonadi, izo zimachitira umboni kuti ine ndakuwuzani inu Choonadi. Iye akadali yemweyo, dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndipo mawonetseredwe a Mzimu Wake akumutengera Mkwatibwi kutali. Lolani chikhulupiriro chimenecho, vumbulutso ligwere mu mtima mwanu, kuti, "*Ili ndilo oralo.*"

Tsopano tiyeni ife tipemphere.

³¹² Wokonedwa Mulungu, Yemwe anawonetseredwa mu thupi mwa munthu wa Yesu Khristu, amene anawuka kwa akufa, tsiku lachitatu, molingana ndi Malemba, ndipo anakwera Kumwamba, ndipo anatuma ophunzira kunjira kuti akaphunzitse dziko lonse lapansi, ndipo anati, "Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira."

³¹³ Mulungu, kwa mpingo wa Chipentekoste wa tsiku lino, kubwezeretsedwa kwa mphatso; mulole, Ambuye, amuna amenewo, mwinamwake ena a iwo omwe ali pano, ena a iwo akumvera tepi kuzungulira dziko lapansi, mulole iwo azindikire kuti uku ndi kuyitanira kunjira kwa Mkwatibwi, osati uthenga wa Chipentekoste. Uthenga wa Chipentekoste unali woti udzabwezeretse mphatso mu Mpingo. Koma uku ndi kuyitanidwa kwa Mkwatibwi, Uthenga wina umene unali woti ubwere Sodomu asanawotchedwe. Aloleni iwo amvetsetse, wokonedwa Mulungu. Chikhulupiriro, ine ndikukhulupirira Izi, chifukwa Izo zawululidwa ndi Mzimu Wanu kudzera mu Mawu a Mulungu ndipo zatsimikiziridwa ndi kuwonetseredwa ku dziko lonse lapansi. Ndithudi, Ambuye, mwa ochepa, nthawi zonse magulu Anu amakhala mwanjira imeneyo. Koma

Inu munati, “Musawope, kagulu kankhosa kakang’ono, ndi chifuniro cha Atate wanu kuti akupatseni inu Ufumu.”

³¹⁴ Koteru, ine ndikupemphera, Mulungu, kuti anthu ayang’ane kutali ndi luntha lawo, ayang’ane kutali ndi zomwe agaganize kuti ndi zolondola, ndipo ayang’ane mu Lemba. Ndipo izo zinayankhulidwa usiku wathawu, aloleni anthu pano aganize monga momwe mfumukazi inachitira mmasiku a chiwonongeko chachikulu cha Babulo, iye anati, “Pali mwamuna pakati panu dzina lake ‘Danieli,’ anali mu ufumu wa atate wanu (Atate achipentekoste, anali mu ufumu wake.) ndipo iye ndi wosungunula wa zokaikira zonse.”

³¹⁵ Ndipo tsopano, Ambuye, mulole Mzimu Woyera umene unali mu ufumu wa chipentekoste, ufumu umene unali wa Marteni Lutera, unali wa John Wesley, ndi—ndi kupitirira mpaka kwa John Smith ndi Alexander Campbell, ndi kutsika kudutsa mu m’badwo. Iye ndi Wosungunula, Iye anasungunula maganizo. Ndipo a—anthu mmasiku a Lutera, munthu ameneyo, “Olungama akuyenera kukhala moyo mwa chikhulupiriro.” Amethodisti, Iye anasungunula kukaikira konse, kuti, “Iwo ayenera—iwo ayenera kukhala oyeretsedwa.” Ndipo mmasiku a Pentekoste, iwo anayankhula mmalirime, kupereka mawonetseredwe a Mzimu mwa machiritso Auzimu ndi zina zotero, Izo zinasungunula kukayikira konse mu mtima wa wachipentekoste. Koma, O Mulungu, iwo anapanga chipembedzo. Iwo anabwerera kumbuyo komwe kunjika kuti akatenge malingaliro a munthu. Chotero, tsopano pamene Mkwatibwi akuyitanidwa monga Inu munalonjeza izo mu Lemba, Kuwerenga Izo pamaso pa dziko, usiku ndi usiku, ndipo ife timaziyang’ana Izo ndi maso athu. Mulungu, mulole Izo zisungunule kukaikira konse mu mtima wa anthu. Mulole iwo athawire msanga kwa Mwana wotseguka, kuti akhwimitsidwe, kuti atengedwere mu nkhekwe ndi kuti asasiyidwe mu phesi kuti awotchedwe, koma mulole iwo apite ku nkhekwe usikuuno. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

Zikomo chifukwa cha tcheru chanu. Mulole Mulungu achite ndi mtima wanu.

³¹⁶ Tsopano, kodi inu . . . Iye tiri nawo makadi apemphero omwe aperekedwa. Tsopano, ife titenga pafupifupi maminiti twente tsopano, kwa mzere wa pemphero. Iye tikufuna kuti tifole mofulumira kwenikweni, ndi kubwera kudutsa nsanja ndi kupemphera. Ndipo tsopano, ine sindikudziwa kuti ndi makadi angati omwe anaperekedwa. Ine sindinamufunse nkomwe Billy chinthu chimodzi. Ine ndinangoti, “Kodi iwe unapereka . . . Pita kumusi uko ndipo ukapereke makadi ena apemphero.” Ndipo iye anabwerera ndipo anakawatenga amayi ake ndi ine ndi iwo, kanthawi kapitako. Tsopano, ine—ine . . . ndinatero . . .

³¹⁷ Chabwino, kodi iwe unayamba ndi handiredi, kapena wani,

ndi wani mpaka handiredi, kapena chiyani? [M'bale Billy Paul akuti, "Wani mpaka thuu handiredi."—Mkonzi.] Wani mpaka handiredi. Chabwino.

³¹⁸ Tiyeni tikhale ndi khadi lapemphero nambala wani. Ngati inu muli nalo ilo, kwezani mmwamba dzanja lanu kuti ine ndikhoze kuwona. Ngati simungathe... Ngati inu mungathe kuyimirira... ngati inu simungathe, ife tidzakunyamulani inu. Khadi la pemphero nambala wani, mwamsanga ndithu. Ndani ali nalo... chiyani—ndi chiyani? A, nambala wani. (Mundikhululukire ine.) A, nambala... Dona uyu apa, kodi inu muli ndi khadi limenero? Bwerani pomwe pano, inu mungatero dona? A, nambala thuu. Kodi inu muli nalo ilo, winawake? Kwezani dzanja lanu msanga. Pomwe pano, dona, bwerani. Nambala firii. Muli ndi khadi? Kodi muli ndi khadi? Nonse inu mulibe makadi, mulibe makadi? Ha? Chabwino, inu simukusowekera kuti mukhale nawo iwo. Firii, foro, faivi. A, wani, thuu, firii, foro, faivi. Tiyeni tiwone, pali wani, thuu, firii, foro, faivi. A... Chabwino, apa iwo... Faivi, sikisi, seveni, eyiti, naini, teni. Chabwino, ingopangani mzere, tangoyambani kufola.

³¹⁹ Tsopano, ngati inu simungakhoze kubwera, gwedezani dzanja lanu monga choncho kotero kuti iwo akhoza kukutengani inu. Ine ndawafunsa anthu awa apa, omwe alibe makadi... Sakusowekera kuti akhale nawo, ine ndikungokufunsani inu. Tsopano penyani, inu—inu anthu olumala pano, ine ndikuganiza iye amayenera kubwera molawirira, chifukwa, iye, ine ndinangomuwuza iye, "molawirira." Tsopano, inu simukusowekera kuti mukhale ndi khadi, ngati inu muli nacho chikhulupiriro chimenecho monga ine ndinaphunzitsira. Mwawona, ngati izo zawululidwa kwa inu, chabwino. Ngati izo sizinawululidwe, ziribe kanthu ngati inu mukhala mmizere ma dazeni ya pemphero, izo sizingathandize mpang'ono pomwe. Inu mukudziwa zimenezo? Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Mwawona? Ine ndikhoza kupemphera, nkuchita zonse zomwe ine ndingakhoze, kugwada pa mawondo anga, ndi kuika manja pa inu, kukudzozi inu ndi mafuta, mulimonse momwe inu mukufunira kutero, ndi kupemphera. Mpaka Mulungu, mwa vum-... mwa chisomo, atawulula zimenezo mu mtima mwanu, "Izo zatha," ndiye izo zatheka. Inu simukusowekera ngakhale kuti mukhale mu mzere kapena paliponse, izo zachitika mulimonse.

³²⁰ Chabwino, foro... Wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni, eyiti, naini, teni, leveni, thwelovu, satini, fortini, fifitini. Chabwino, sikisitini, seventini, eyitini, naintini, twente. Kodi alipo amene ndamuyitana yemwe ali ndi khadi ndipo sangathe kuyimirira? Kwezani dzanja lanu, muli ndi khadi ndipo simungathe kuyimirira. Chabwino.

... kungo khulupirira,

Ine ndikukhoza kumuwona wosauka, wamng'ono, Anna Jeanne wokalama atakhala, akusewera iyo usiku wonse, pafupifupi, nthawi. Ine ndikufuna aliyense mwakachetechete kwenikweni ndi molemekeza, monga inu mukudziwa.

...kungo khulupirira;

Tsopano, makadi apemphero wani mpaka fifitini, ine ndikukhulupirira anali.

...kungo khulupirira,

Iwo akuyamba kudzadzana pang'ono pano, kotero tiyeni—tiyeni tingoyamba. Nanga inu mukuti bwanji?

...zotheka...

³²¹ Wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni, eyiti, naini, teni... Tsopano, mukuyamba kuchulukana kwambiri. Ndiwo ambiri kuposa omwe ife tinayitana. Izo zonse nzabwino. Imani njii, basi pomwe inu muli. Osati munthu basi...inu mupeza...Inu mumapemphereredwa, koma basi...Mwawona, ingodikirani mpaka iwo ayitane nambala yanu. Ndiye, inu mukudziwa, ife—ife tiribe ochuluka omwe ayimirira pano. Ngati Ambuye akanati achite chinachake, inu mungachitchingire icho kwa anthu ndipo iwo sangakhoze kuchiwona icho, inu mwawona. Mulungu akudalitseni inu.

Tsopano tiyeni tipempherere mipango iyi pamene iwo akukonzekera.

³²² Wokonedwa Mulungu, apa pali mipango ili apa yomwe ikuchokera kwa odwala ndi osautsika. Chikhulupiriro ichi chimene ife takhala tikuchikamba kumene, Ambuye; Ine ndikukumbukira Inu mukunena, mu Baibulo, mu Bukhu la Yuda, “Mowonamtima limbanirani chikhulupiriro chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera mtima.” Ndipo kuchokera mu thupi la oyera mtima iwo anatenga mipango, osati chifukwa iwo anali anthu apadera, koma chifukwa iwo anali anthu okhulupirira. Iwo anali anthu a cholinga chofanana monga ife tiliri. Iwo anati, “Eliya” anali choncho ndipo iye “anapemphera mowonamtima kuti mvula isavumbe.” Ndipo, Mulungu, iye anapempherera *chimenecho* kotero kuti anthu alape. Inu munawulula izo kwa iye kuti awapempherere iwo, kupemphera mwa njira imeneyo kuti mukwaniritse Mawu Anu. Ndi zosakaikitsa Inu munamuwonetsa mneneriyo masomphenya. Ndipo, Ambuye, usikuuno ndikuwapempherera anthu awa kuti achiritsidwe. Ine sindine Eliya, iye anatengedwera Kumwamba, koma Moyo wake ndi Mzimu zikukhalabe moyo. Kotero ife tikupemphera, Mulungu wokonedwa, kuti Inu mulemekeze mapemphero a anthu Anu. Ndipo lemekezani ife tonse tsopano pamene ife tizipempherera mipango iyi, kuti pamene iyo ikaikidwa pa odwala iwo akachire.

323 Ife tikuzindikira, Atate, kuti ndife a—m’badwo wakufa wa anthu. Ife tikulunjika . . . kukumanizana—kukumanizana ndi Umuyaya. Dziko lachita misala. Kuphana; atsikana aang’ono akudulidwa mzidutswa ndi kuwonongedwa. Anthu, amuna ovala tsitsi lawo monga akazi, akazi monga amuna, iwo akungopotoza. Mtundu ukufa. Dziko likufa. Zonse zikufa. Mpingo ukufa.

324 O Mulungu, bweretsani Moyo. Bweretsani Moyo, O Mulungu, Moyo wa chikhulupiriro. Wululani kwa anthu awa, Ambuye. Ine ndikhoza kungopemphera ndi kusanjika manja anga pa iwo. Koma Inu ndinu Mmodzi yemwe mungakhoze kuwachiritsa iwo, ndipo Inu nokha mukhoza kuwachiritsa iwo. Ine ndikupemphera kuti Inu mutero, Atate, kwa wina aliyense. Perekani izi, ndi manja anga pa iwo, ndi kupempha ndi mtima wanga wonse; mu Dzina la Yesu Khristu, achiritseni anthu awa. Amen.

325 Tsopano, kodi choyankhulira ichi chiri moyo, M’bale? Tsopano kodi inu mukumva zimenezo bwinobwino? Aliyense akumva zimenezo? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino. Tsopano, mwanjira ina kapena inzake, mtima wanga ukupita kwa anthu awa pano, akhala apa mu uwu—mpando uwu, zikuku ndi machira . . . iwo “sanapeze ngakhale khadi lapemphero.” Mwawona? Koma, tayang’anani, m’bale, mwawona, anthu awa ali ndi makadi apemphero, koma izo sizikutanthauza kuti iwo achiritsidwa. Pali anthu akhala kunja uko mwa omvetsera, mwina, zimenezo—zimenezo—zimenezo sizikutanthauza kuti iwo ali—iwo—iwo achiritsidwa. Kuti—izo sizikunena kuti—kuti iwo adzachiritsidwa kapena sadzachiritsidwa. Izo zonse zimadalira pa chikhulupiriro chawo mwa Mulungu. Ndi angati akudziwa kuti izo ndi zoono? Ndizo zonse, basi chikhulupiriro chawo mwa Mulungu. Chabwino, tsopano, ndi angati akudziwa kuti izo nzoona? Ziribe kanthu kaya ndinu wachipembedzo motani, ndinu wabwino kapena woyipa motani, pokhapokha chisomo cha Mulungu chigwetsere izo mu mtima mwanu, inu simudzakhala bwino konse. Tsopano, ndi angati akudziwa kuti Mulungu wazichita izo, wazichita izo nthawi yonse, zozizwitsa zazikulu, zizindikiro ndi zodabwitsa? Ndipo tsopano, inu mukubwera usikuuno, kuyimirira pamzere uwu, osati chifukwa munasankhidwa kuti muyime mu mzere uwu ndi Mulungu, izo si zimenezo; inu mwangolandira khadi la pemphero, munangopezeka kuti muli kwanu. . . [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

326 Ndongomeko ndi basi ndendende monga M’bale wanga wolemekezeka Hierholzer pano, anayamba utumiki wake zaka zambiri zapitazo. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] . . . ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, akukhulupirira Mulungu, akukhulupirira kuti Mulungu anachiritsa odwala mwa chikhulupiriro. Ndipo izo sizinasinthe konse, koma Mulungu wawonjezera mu tsiku lotsiriza lino, mphatso, mphatso zimene

Iye analonjeza. Mulungu anachita izo chifu-. . .osati chifukwa Iye ankayenera kutero, koma chifukwa Iye analonjeza kutero. Ndipo ngati Iye analonjeza, ndiye Iye akuyenera kuti achite izo; chifukwa Iye akuyenera kusunga Mawu Ake.

³²⁷ Ndipo Iye anakulonjezani inu chinthu chomwecho, ndiko kuti, “Ngati inu mukanakhoza kukhulupirira, kuti izo zikanachitika; ngati inu simungakhulupirire izo, izo basi sizichitika.” Tsopano, ine sindingakupangitseni inu kuti mukhulupirire, inunso simungadzipangitse nokha kukhulupirira. Mulungu akuyenera kuti apereke izo kwa inu. Ndi mphatso ya Mulungu, kuti mukhulupirire. Osati chikhulupiriro chanu, chikhulupiriro cha Mulungu. Chikhulupiriro chanu chaluntha chikhoza kukhulupirira izo bwino, koma pokhapokha chikhulupiriro cha Mulungu chiri pansu mu mtima mwanu. . .Mwawona, chikhulupiriro chanu chaluntha chikhoza kuzilandira izo, kuchita izo. Ndipo mungopitirira kuzikhulupirira izo ndi mtima wanu wonse mpaka Mulungu atawulula izo kwa inu. Mukuwona? Zingopitirirani kuzikhulupirira izo mpaka Mulungu ataziwulula izo. Koma mpaka Iye ataziwulula izo. . .

³²⁸ Inu mukuti, “M’bale Branham, kodi inu mukuti chiyani pamenepo?”

³²⁹ “Inde, bwana!” Mulungu anatumiza mneneri kwa Hezekiya ndipo anamuuza iye, “‘Iwe siuchoka pa bedi limenero,’ PAKUTI ATERO AMBUYE. ‘Iwe ufera pamenepo pabedi limenero.’” Kulondola uko?

³³⁰ Koma mneneri ameneyo anatembenuka. . .kapena mfumu imeneyo inatembenezira nkhope yake kukhoma, ndipo inalira ndi misozi yowawa, ndipo inati, “Ambuye, ine ndikusowekera zaka zina fifitini. Ine ndikukudandaulirani Inu, Ambuye, kuti mundimve ine.” Tsopano, mfumuyo inali munthu wamkulu kwambiri mu dziko lapansi, mu ndale; koma, mneneriyo anali, pamaso pa Mulungu. Imeneyo inali mfumu ya Mulungu; koma uyo anali mneneri wa Mulungu. Koteri, Mulungu anawulula kwa mneneri kuti atenge zina. . .awiritse zina. . . [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Inu mukudziwa, mukumvetsista?

³³¹ Tsopano, kuti inu mukhoze kumvetsetsa tsopano, chifukwa ine ndalalikira Malemba pano, “Monga izo zinaliri mmasiku a Sodomu, momwemonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu.” Mmasiku amene mpingo uzidzawululidwa? Ayi! “M’masiku amene Mwana wa munthu adzawululidwa.” *Kuwululidwa* ndi chiyani? Kupangidwa kudziwika! Kulondola uko? Kuwulula! Tsiku limene Mwana wa munthu adzawululidwa, lidzakhala tsiku ngati Sodomu ndi Gomora. Ndi kulondola uko?

³³² Tsopano, tayang'anani chimene chinachitika. Iwo anali nawo amithenga aakulu awiri, kumusi uko mu Sodomu ndi Gomora, chifukwa kunali gulu la Akhristu ofunda kumunsi kumeneko. Ndi kulondola uko? Ndipo iwo anali nawo amithenga aakulu awiri (tsopano mvetserani mwacheru) uko mu Sodomu ndi Gomora, akulalikira. Koma mmodzi wa iwo amene anayima kunja kuno ndi gulu la Abrahamu. Kulondola uko?

³³³ Tsopano penyani! Ife sitinayambe, mu mbiriyakale yonse ya mpingo, sitinayambe takhalapo naye wamthenga wa dziko lonse kwa mpingo amene dzina lake linkathera mu h-a-m, kufikira tsopano: G-r-a-h-a-m, zimene ziri zilembo sikisi, G-r-a-h-a-m. Koma dzina la Abrahamu linkatchulidwa: A-b-r-a-h-a-m, zilembo seveni. Mwawona? Chotero mpingo wa dziko lonse, pokhala chilembo cha munthu, sikisi, bungwe lopangidwa ndi anthu, komabe walandira wamthenga wawo. Iwo akhala naye Sankey, Moody, Finney, Knox, Calvin, ena otero, koma osati "h-a-m." Ndi kulondola uko? Koma iwo ali naye iye, ndipo iye ndi wamthenga, wotumizidwa kuchokera kwa Mulungu, ndipo iye akugumula makoma amenewo mwamphamvu momwe iye angathere, "Chokani muno! Lapani kapena muwonongeka!"

³³⁴ Koma kumbukirani, Wosankhidwa, wokonzedweratu, pangano lokhazikitsidwiratu, Abrahamu ndi gulu lake, anali naye Mtumiki, nawonso. U-nhu. Penyani chimene Iye anachita. Iye anawapatsa iwo chizindikilo chakuti nthawi inali pafupi yakuti moto ugwe. Tsopano, ndi moto tsopano umene ife tikuwuyembekezera, moto wa atomiki, mkwiyo wa Mulungu.

³³⁵ Tsopano, Wamthenga ameneyo anachita chinachake. Iye anayankhula za mkazi yemwe Iye anamutembenezira nsana Wake, ndipo anamuwuza iye—ndipo anamuuza iye kuti iye ankakaikira chimene Iye ankanena, anamuuza iye zikhalidwe zake ndi zimene zinkati zidzachitike. Ndi kulondola uko? Kodi Iye ananena kuti Mwana wa munthu akanadzadziwulula Yekha mwanjira yomweyo mu tsiku limenero? Chabwino, kodi inu mukukhulupirira zimenezo ndi Choonadi?

Chabwino, apa payima mkazi, . . .

³³⁶ Ndipo mu chilumikizano chosawoneka cha Mpingo, Mkwatibwi kwa Khristu, Wamthenga ameneyo ali pano tsopano, amene ali Yesu Khristu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

³³⁷ Tsopano, Iye amayankhula kudzera mwa aneneri Ake okha. Baibulo linanena chomwecho! "Iye sachita kalikonse koma poyamba Iye amazipanga izo kudziwika kwa aneneri Ake," Amosi 3:7. Iye nthawizonse wazichita izo. Iye samasintha konse kachitidwe Kake. Mukuwona? Ndipo mneneri akhoza kokha kuyankhula, ngati iye ali woona, chimene Mulungu akumuwuza iye. Ndi kulondola uko? Ndizoona.

338 Tsopano, kodi inu mukukhulupirira kuti Iye akhoza kundiwuza ine chomwe chiri vuto ndi mkazi uyu ine ndisanamuyang'ane nkomwe iye? Kodi inu mukukhulupirira izo? Bwanji, iye akuvutika ndi khansa. Uko nkulondola. Ili pa bere lake. Iye ali ndi mnyamata, mmalingaliro ake, iye akuvutika ndi mtundu wa chikhalidwe cha misala, chikhalidwe cha manjenje, ndi zosokonekera. Uko nkulondola. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ndipo izo ndizowona, sichoncho izo? Kodi inu mukukhulupirira tsopano kuti chikhulupiriro chanu, ndi kunena zimenezo, chazikika, kuti inu muli nacho icho, inu mukhala nacho icho? Ndiye pitani, ndipo Ambuye Yesu akuchizani inu. Mukuwona? Eya. Mwawona? Kodi inu mukukhulupirira? Ndi mtima wanu wonse?

339 Tsopano, kodi inu mukukhulupirira, popanda kuyang'ana pa mkazi uyu, Ambuye Yesu akhoza kundiwuza ine lomwe liri vuto lake? Ndi angati akukhulupirira zimenezo? Tsopano, inu mukudziwa...ndipo sindinayambepo ngakhale...Ine... chinthu chokhacho, ine ndinangowona siketi. Ine sindikudziwa, sindimadziwa ngati anali mwamuna kapena mkazi; koma kungoyima pamenepo. Ine ndikufuna iye kuti akhulupirire. Kodi inu mukukhulupirira, dona? Pano, wodwala, kodi inu mukukhulupirira? Kwezani mmwamba dzanja lanu ngati inu mukukhulupirira. Ngati inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kukhala ndi mwana ameneyo yemwe inu mukumupempha Mulungu. Mwawona? Mwawona? Inu mukukhulupirira? Inu muli ndi chikhulupiriro mwa Mulungu? Tsopano, zimenezo sizimachiritsa, zimenezo zangozindikiritsidwa. Ndizo ntchito zimene zimazindikiritsa chikhulupiriro cha Kukhalapo kwa Mulungu, Mawu Ake akuwonetseredwa.

340 Mkazi uyu akufuna chinthu chachikulu, nayenso. Ameneyo si mwana, koma iye akufuna Ubatizo wa Mzimu Woyera. Ine ndikuwuzani inu choti muchite: Ngati inu muti muchotse ndudu zimenezo, Mulungu adzakupatsani inu Ubatizo wa Mzimu Woyera. Pitani, mukhulupirire Izo, mwawona. Kodi inu mukukhulupirira? Kodi inu muli ndi chikhulupiriro mwa Mulungu?

341 Mwamuna uyu wayima apa, ndi mwamuna yemwe ine sindinayambe ndamuwonapo mmoyo wanga. Ine sindikumudziwa iye, koma iye akuvutika ndi chinachake cholakwika mu chifuwa mwake. Iye anali ndi kugwa kumene kunachita zimenezo, osati kale kwambiri. Iye si wochokera kuno, iye akuchokera ku Arkansas. Iye ndi mlaliki. Pitani kwanu, kalalikiireni Uthenga. Mwawona? Mwawona? Mwawona? Ine sindinayambe ndamuwonapo munthuyo pa nkhope yake.

342 Pali mkazi wayima apa, ine sindikumudziwa mkaziyo, sindinamuwonapo iye mmoyo wanga. Mulungu akumudziwa iye.

343 Ngati Iye angakhoze kuwulula lomwe vuto lake liri, kapena chinachake cha izo, kodi inu mungakhulupirire? Nonse a inu? Iyi ndi ntchito yokha ikuzindikiritsa chikhulupiriro chimene ine ndiyenera kuti ndilalikire chimene ine ndakuwuzani inu, usikuuno. Ndicho chimene Mulungu anachiwulula, ndipo izi ndi ntchito zikutsimikizira Izo. Tsopano, inu mukuyenera kuti mukhale nacho chikhulupiriro kuti mukhale bwino.

344 Mkazi uyu apa, ine sindikutero—ine sindikuganiza kuti ine ndikumudziwa iye. Inde, ine sindikumudziwa iye koma ine ndikumudziwa winawake yemwe iye akumudziwa, chifukwa ine ndikumuwona iye atayima pano patsogolo panga. Iye akuvutika ndi kupweteka kwamutu. Si choncho, dona? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchiritsani inu? Mlono wa Peary Green. Uko nkulondola. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye mmoyo wanga. Uko nkulondola. Ine ndinamuwona Peary Green atayima apa, akuyang'ana pa ine, akupita monga *choncho*. Ingobwerani, mwawona. Kulondola. Ine sindikudziwa komwe Peary Green ali. Kodi inu mukukhulupirira? Kodi inu mukukhulupirira mochuluka bwanji? Ngati inu mungakhoze kukhulupirira, zinthu zonse ndi zotheka. Ngati inu simungakhoze kukhulupirira, palibe chomwe chingachitike.

345 Dona wamng'ono wa tsitsi la imvi, wakhala apo akuyang'ana pa ine, pomwe pano, kodi inu mukumukhulupirira Mulungu? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuwulula kwa ine zomwe inu mukuziganizira pamenepo? Muli ndi chotupa pa bere. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kukuchotserani inu icho? Inde. Khalani ndi chikhulupiriro ndi kukhulupirira. Tsopano, kodi iye anakhudza chiyani?

346 Mkazi amene anakhudza mphonje ya chovala Chake, Baibulo linati. . . Inu amene mukufuna kuti mutenge Baibulo, Iye anati, “Iye ndi Mkulu Wansembe amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zofooka zathu.” Kumeneko si kulondola? Iye ndi Mkulu Wansembe uja ndipo Iye wayima pomwe pano; anthu amenewo akumukhudza Iye.

347 Pali mkazi wamng'ono, wowonda, anakweza mmwamba dzanja lake, wakhala pomwe pano. Ine sindinamuwonapo iye mmoyo wanga, koma iye basi pamenepo anakhudza Chinachake. Izi ndi zomwe zinali. Iye akupemphera kwa Mulungu. Iye ali ndi vuto mu chifuwa mwake, iye alinso ndi vuto la mmimba. Mulungu anakuchiritsani inu, ngati inu muti mukhulupirire Izo. Inu muyenera kukhulupirira. “Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira.”

348 Pali mwamuna wakhala kumbuyo uko kumbuyo, akuyang'ana mbali iyi (pafupifupi mzere wachiwiri, kubwera mbali iyi), akuvutika ndi mphumo. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchiritsani inu, bwana? Ngati

inu mukukhulupirira Izo, Mulungu akupangani inu wabwino. Inu mukhoza kukhala nacho chimene inu mwachipempha, ngati inu mukukhulupirira Icho.

³⁴⁹ Pali mkazi wakhala pomwe pano, akundiyang'ana ine, cha apa, wamutu wa imvi. Ngati inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse. . . Kodi inu mukukhulupirira Izo? Chabwino, vuto la ndulu ilo likusiyani inu ndiye, ngati inu mukukhulupirira Izo.

³⁵⁰ Kodi inu mukuganiza chiyani za Izo, mwagona apa pa chikuku? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kukuchiritsani inu? Ngati Mulungu angandiwuze ine vuto lanu, kodi inu mumukhulupirira Iye? Ngati inu mukhulupirire, khansa imeneyo ikusiyani inu ndipo inu mukhala bwino. Bwanji inu osayimirira, ndi kutenga mphasa yanu, ndi kumapita kwanu? Kodi inu mukukhulupirira? Kodi nonse a inu mukhulupirira? Chabwino, tsopano, nanga bwanji pakali pano? Kodi Mulungu wagwetsera chikhulupiriro chimenecho mu mtima mwanu? Aliyense muno, kwezani dzanja lanu. Ngati Mulungu wagwetsera chikhulupiriro chimenecho mu mtima mwanu, tiyeni muyike manja anu pa wina ndi mzake, mmusi momwe cha mumzere apa. Ikani manja anu. . . Pakali pano, mwamsanga, pamene Mzimu Woyera ukuyenda, ikani manja anu pa wina ndi mzake. Bamboyo wadzuka, akuthamanga pansu pa mzere, akupempherera ena.

³⁵¹ Tiyeni tiyime pa mapazi athu ndi kupereka matamando kwa Mulungu, aliyense. Palibe chifukwa choti tipite motalikira. Mumuzindikiritse Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Inu, chimene kusautsika kwanu kuli, chirichonse chimene icho chiri, ngati inu mukumukhulupirira Iye, imani pa mapazi anu, pakali pano, ndipo khulupirirani.

³⁵² Mulungu Wamphamvuzonse, Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isaki, Mulungu wa Yakobo, tumizani mphamvu Yanu ndi kuchiritsa gulu ili la anthu pakali pano, mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

Ulemerero ukhale kwa Mulungu! Mulungu akudalitseni inu.



65-1126 Ntchito Ndi Chikhulupiriro Chofotokozedwa
Life Tabernacle
Shreveport, Louisiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org